# CHENJEZO LOOPSYA LA ALLA

**BISMILA-HIR RAIJANIR RAHIM** Assalamu' Alaikum!

**Za m'kabukhu'ka: Chisilamu mu Ulosi wa M'Bukhu Lopatulika - Ismayeli, Komwe Anachokera ndi Madalitso ake - Anthu a Maiko a Kum'mawa - Yesu m' Korani Wolemekezeka - Chisilamu ndi Mpingo Wakukonzanso Wa Mpanduko - Kodi akufa amalankhulana ndi amoyo? - Dzombe, monga khamu lalikuru la ankhondo a Mulungu - Uthenga wa Angelo Atatu - Chilembo cha Chirombo - Dziko la Mgwirizano la America wa Kumpoto - Kodi Akhristu onse ndi ofanana? - Nanga ndi ndani anasintha malamulo a Mulungu? - Minda ya Myaya - ndi zina...**

**Ili ndi chenjezo loopysa ngati linaperekedwapo m'nthawi ya Nowa, pamene anatumidwa kukhoma chingalawa chomwe anthu osankha koyenera anapulumukiramo. Nowa anatumidwa kuchenjeze osalungama m'dziko lonse, asiye machimo natembenukire kwa Mulungu Mlengi wamoyo. Uthenga wa chilango cha chigumula cha madzi unali chenjezo kwa anthu amene anakhala m'dziko lomwe linakutidwabe m'ulemelero ndi kukongola kwake kwa pachilengedwe. "Ife tinatumiza Nowa kwa anthu a m'badwo wake, ndipo analalikira pakati pao zaka chikwi chimodzi kuchotsapo makumi asanu: koma chigumula chinaononga onse amene (anakakamirabe mu) uchimo." Sura 29. 14 Al Ankaboot.**

**Okondedwa, tiri m'nthawi yotsiriza ya dziko lapansi, yomwenso ndi ya chenjezo lotsindika – lochititsa mantha lomwe likuperekedwa komaliza – lilalikidwe kwa anthu okhala m'dziko. Kodi uthenga wakuchenjezawu ndi woti chiyani? Ndani akuulalikira? Tingakonzeke motani kuti miyoyo yathu iulandire?**

**Tidzipempherа kwa Mulungu kuti "atiоnetsere njira ya chilungamo." Qur'an Sura 1.6 Al-Fatiha.**



**Tisanalowe mkati mwa Uthenga Wakuchenjeza kwakukuru'wu wa ngati womwe unaperekedwapo nthawi ya Nowa [Nuh], tiyambe tamvetsetsa bwino mbiri ya Chisilamu, monga yalembedwa m'Mabuku Oyera.**

## MBIRI YA CHISILAMU M'BUKHU LOPATULIKA

Kodi ndi zoona kuti mbiri ya Chisilamu inalembedwa m'Bukhu Lopatulika? Monga Mohammed ndi mneneri wochokera ku chipululu amene m'masamba oyera a Bukhu Lopatulika munalembedwa za iye? Ngakhale mafunso awiriwa ndi mayankho ao, angadzutse mkwiyo wa anthu ena, koma Malemba ouziridwa ndi Mzimu wa Mulungu akunenetsa kuti yankho la onsewo ndi "Inde." Tigwiritsa ntchito mau a m'Mabuku Oyera a Bukhu Lopatulika kuti timvetsetse chomwe watibvumbulutsira Mulungu. Patsogolo pa zonse, tipemphere kuti Mulungu atitsogolere m'njira ya choonadi.

"Mulungu…amatsogolera m'njira ya chilunjiko…" Sura 2.26 Al-Bagara.

Mobwerezabwereza Qur'an Lolemekezeka limalozera woliwerenga ku Mabuku Oyera omwe analembedwa ilo lisanakhale, momwe mukupezeka malangizo, kuunika, kulekanitsa pakati pa chabwino ndi choipa ndiponso machenjezo. Ndi ku machenjezowa komwe titembenukire kupezeko chidzwitso.

"Ndife tinabvumbulutsira chilamulo (kwa Mose): momwe muli chitsogozo ndi kuunika. M'chilamulocho, Ayuda anaweruzidwa, ndipo kudzera mwa aneneri omwe anagonjera… chifuniro cha Mulungu, ndiponso mwa aphunzitsi ndi akachenjede a chilamulo: kwa iwo kunapatsidwa mphamvu yakulitchinjiriza bukhu la Mulungu… Ndipo pambuyo pa awa **Tinatumiza Yesu Mwana wamwamuna wa Mariya, kudzachikhazikitsa chilamulo chimene chinakhala iye asanabadwe:** Tinampatsa Uthenga Wabwino: momwe muli malangizo ndi kuunika. Ndiponso chikwaniritso cha chilamulo chomwe chinaperekedwa asanadze iye; chokhala ndi malangizo ndiponso chidzudzulo kwa onse akuopa Mulungu." Sura 5.44, 46 Al-Maeda.

"Ndipo kumbukirani **Ife tinampatsa Mussa Malemba Oyera ndi Muyeso wakulekanitsa (chabwino ndi choipa)…"** Sura 2.53 Al-Baqara.

## MAGWERO A CHISILAMU

Mbiri ya chiyambi cha Anthu a Maiko a Kum'mawa ikupezeka m'Taurat. Mibadwo, mapfuko ndi chiyambi cha Chisilamu zinayambira nthawi ya Abrahamu ndi mwana wake woyamba kubadwa Ismayeli. Ismayeli anali mwana wa Abrahamu mwa Hagara ( mlendo), chifukwa anali m'Aigupto nalinso mdzakazi wa Sarai, mkazi wa Abrahamu.

Kufotokoza Mwachidule: Mulungu analonjeza Abram ndi mkazi wake Sarai kuti adzakhala ndi mwana wamwamuna, koma lonjezanolo linachedwa kukwanitsidwa. Itadutsa nthawi yaitali osalandira mwana wolonjezedwayo, Abrahamu anataya mtima nakhumudwa, nakufika podandaulira Mulungu.

"Ndipo Abramu anati, Ambuye Mulungu, mudzandipatsa ine chiyani popeza ndine wopanda mwana….?" Taurat Genesis 15:2.

Ndipo Ambuye anayankha Abramu nati, "…koma iye amene adzaturuka m'chuuno mwako, ndiye adzakhala wakulowa m'malo mwako." Taurat Genesis 15:4

Lonjezano'li linali lotsimikizika, ngakhale linatenga nthawi kukwanitsidwa.

## KUBADWA KWA ISMAYELI NDI ISAKE

Zolembera izi zikufotokoza chosayenera chomwe Abramu ndi Sarai, anachichita posafunsira chitsogozo cha Mulungu ngati kunali koyenera kuti Abrahamu adzipangire yekha mlowa m'malo wake kudzera mwa mkazi wina.

"Ndipo Sarai mkazi wake wa Abramu sanambalire iye mwana; ndipo anali ndi mdzakazi, wa ku Aigupto, dzina lake Hagara. Ndipo Sarai anati kwa Abramu, Taonanitu, Yehova anandiletsa ine kuti ndisabale: lowanitu kwa mdzakazi wanga; kapena ndikalandire ndi iye ana. Ndipo Abramu anamvera mau a Sarai. Ndipo Sarai mkazi wake wa Abramu anatenga Hagara mdzakazi wake wa ku Aigupto, , nampereka iye kwa Abramu mwamuna wake, kuti akhale mkazi wake. (Ichi chinachitika Abramu atakhala m'Kanani zaka khumi).

"Ndipo analowa kwa Hagara, ndipo iye anatenga pakati. Pamene anaona kuti anatenga pakati, [Hagara] anapeputsa wakuka wake [Sarai] m'maso mwake. Ndipo Sarai anati kwa Abramu, Kusauka kwanga kukhale pa iwe… Yehova aweruze pakati pa iwe ndi ine.

"Abramu anayankha Sarai nati, Taona mdzakazi wako ali m'dzanja lako, umchitire iye chimene chikukomera m'maso mwako. **Ndipo Sarai anamsautsa iye, ndipo anathawa kumaso kwake.**

"Ndipo mthenga wa Yehova anampeza iye pa kasupe wa madzi m'chipululu, pa kasupe wa pa njira yaku Suri. Ndipo anati, "Hagara, mdzakazi wake wa Sarai, ufumira kuti? Ukunka kuti?

"Ndipo anati, Ndithawa ine kumaso kwake kwa wakuka wanga Sarai. Ndipo wamthenga wa Yehova anati kwa iye, **"Bwerera kwa wakuka wako, udzichepetse wekha pamanja pake."** Ndipo wamthenga wa Yehova anati kwa iye, 'Ndidzachurukitsa ndithu mbeu zako, kuti unyinji wao sudzawerengeka.'

"Ndipo mthenga wa Yehova anati kwa iye, …udzabala mwana wamwamuna; **nudzamutcha dzina lake Ismayeli (kutanthauza kuti Mulungu amamva),** chifukwa Yehova anamva kusauka kwako. Ndipo iye adzakhala munthu wa mthengo; ndipo dzanja lake lidzakhala lotsutsana ndi anthu onse ndi manja a anthu onse adzakhala otsutsana naye. Adzakhala ndi kuonetsa udani waukuru pa abale.

"Ndipo pomwepo Hagara anamtcha Yehova amene analankhula naye, "Ndinu Mulungu wakundiona ine; pakuti anati, 'kodi kunonso ndayang'ana pambuyo pake pa Iye amene wakundiona ine?' Chifukwa chake chitsime cho chinatchedwa Beerelahai-roi (kutanthauza 'ubwino wa Iye Wakukhala ndi moyo yemwe akundiona ine'). Chitsimechi chiripobe mpaka lero ndipo chiri pakati pa Kadese ndi

Berede.

"**Ndipo Hagara anam'balira Abramu mwana wa mwamuna ndipo Abramu anatcha dzina la mwana wake amene anambalira iye Hagara, Ismayeli**. Ndipo Abramu anali wa zaka makumi asanu ndi atatu kudza zisanu ndi chimodzi, pamene Hagara anambalira Abramu Ismayeli." Taurat Genesis 16: 1-16 NLT.

Zitapita zaka khumi ndi zitatu, Mulungu anabwerezanso pangano analipangana ndi Abramu, ndi kumtsimikizira kuti adzakhala "tate wa makamu a amitundu" ndi wa mtundu waukuru "ndidzakuchurukitsa iwe koposa." Pomwepo Mulungu anasintha dzina la Abramu kukhala Abrahamu (ndiponso Sarai kukhala Sara) chitsimikizo cha pangano analichita'lo.

Ismayeli anaikidwanso m'pangano la Mulungu, lomwe chitsimikizo chake chinali mdulidwe, monga mwa chifuniro cha Mulungu. "Ndipo Mulungu anati kwa Abrahamu, Koma iwe, uzikumbukira pangano langa, iwe ndi mbeu zako pambuyo pako m'mibadwo yao. 'Ili ndi pangano langa limene uzisunga pakati pa Ine ndi iwe ndi mbeu zako pambuyo pako: azidulidwa amuna onse a mwa inu. **Mudzidula khungu lanu; ndipo chidzakhala chizindikiro cha pangano pakati pa Ine ndi inu.'"** Taurat Genesis 17:9-11 TNIV

"Ndipo Abrahamu anatenga Ismayeli mwana wake ndi onse amene anabadwa m'nyumba mwake, ndi onse amene anagulidwa ndi ndalama zake, amuna onse a mwa anthu a kunyumba kwake kwa Abrahamu, nadula khungu lao tsiku lomwelo, monga Mulungu ananena naye. Ndipo Abrahamu anali wa zaka makumi asanu ndi anai kudza zisanu ndi zinai, pamene anadulidwa m'khungu lake. Ndipo Ismayeli mwana wake anali wa zaka khumi ndi zitatu pamene anadulidwa m'khungu lake. Tsiku lomwelo anadulidwa Abrahamu ndi Ismayeli mwana wake." Taurant Genesis 17:23-26 TNIV. Pangano lokhala ndi mdalitso'li ndiponso kumvera monga njira yolilandirira, linaperekedwa **Isake asanabadwe.**

"Chaka chinacho, Abrahamu anakwanitsa zaka 100 ndi Sara analinso wokalamba, Mulungu anakwaniritsa pangano lake lodabwitsa'lo. Sara, anakhala ndi pakati, chinthu chomwe m'chikhalidwe cha umunthu chinali chosatheka kuti munthu wokalamba chotere chimchitikire.

"Ndipo Yehova anayang'anira Sara monga momwe anati, ndipo Yehova anamchitira iye monga ananena. Ndipo Sara anatenga pakati, nam'balira Abrahamu m'ukalamba wake mwana wamwamuna, nthawi yomweyo Mulungu anamuuza iye. Ndipo Abrahamu anamutcha dzina lake la mwana waoyo, Isake. Ndipo pakupita kwa masiku asanu ndi atatu kuchokera pomwe Isake anabadwa, Abrahamu anamdula m'khungu iye monga analamulira Mulungu… Ndipo Sara anati, Mulungu anandisekeretsa ine; onse akumva adzasekerera pamodzi ndi ine. Akadatero ndani kwa Abrahamu kuti Sara adzayamwitsa ana? Pakuti ndam'balira iye mwana wamwamuna m'ukalamba wake!" Taurat Genesis 21:1-7 TNIV

## KULEKANITSIDWA KWA ISMAYELI NDI ISAKE

Pamene Isake anakula nasiyitsidwa kuyamwa, Abrahamu anakonza phwando lalikuru kukondwerera kuleketsedwa kuyamwa kwa mwanayo. Pamene Sara anaona Ismayeli, mwana wa mdzakazi wake, Hagara wa chi-Aigupto, akusowetsa mtendere Isake, anatembenukira kwa Abrahamu nati, "Chotsa mdzakazi uyo, ndi mwana wake wamwamuna; chifukwa mwana wa mdzakazi uyo sadzalowa m'nyumba pamodzi naye mwana wanga Isake. Zosatheka!

"Ndipo mauwo anamuipira kwambiri Abrahamu chifukwa Ismayeli anali mwana wake yemwe anamkondanso kwambiri. Ndipo Mulungu anati kwa Abrahamu, Usaipidwe nao [mau'wo], chifukwa cha mnyamatayo, ndi chifukwa cha mdzakazi wako; momwe wakuuzira iwe Sara umvere iwe mau ake; chifukwa kuti mwa Isake zidzaitanidwa mbeu zako. Komanso ndidzapanga mtundu waukuru kuchokera mwa ana a mwana wamwamuna wa Hagara'yo chifukwa iyenso ndi mwana wako.

"Ndipo Abrahamu anadzuka m'mawamwa tsiku lotsatira, nakonza chakudya ndi chotengera madzi, nadzipachika izi pa mapewa a Hagara. Ndipo anamuuza iye achoke ndi mwana wao; ndi Hagara anayendayenda m'chipululu cha Beseba osadziwa koti alowere. Pamene madzi akumwa anatengawo anatha, anamkhazika mwana wake pansi pa mthunzi wachitsamba. Ndipo iye anachoka nakhala pa mtunda wotalika muyeso zana limodzi nati, 'Sindifuna kuona mnyamatayu akufa.' Iye analira mokweza mau kwinaku akukhetsa misozi.

"Mulungu anamvanso kulira kwa mnyamatayo, ndipo mngelo wa Mulungu kuchokera kumwamba anapfulira Hagara nati, Watani Hagara? Usaope! Chifukwa Mulungu anamva mau a mnyamata kumene ali. Tanyamuka, kukamtonthoza iye, chifukwa mwa mbeu zake ndidzapanga iye mtundu waukuru.

**"Ndipo Mulungu anatsegula maso a Hagara, ndipo iye anaona chitsime chodzala ndi madzi.** [Ichi ndi chitsime chomwe kuyambira pomwepo chakhala chikutchedwa chitsime cha Zamzam. Hagara mofulumira anadzadza madzi mchotengera anali nacho napatsa mnyamatayo amwe. Ndipo Mulungu anakhala ndi mnyamatayo nthawi yonse yakukula kwake m'chipululu. Mnyamatayo anakhala katswiri wosaka ndi mauta, nakhazikika m'chipululu cha Parana. "Ndipo amake anamtengera iye mkazi wa ku dziko la Aigupto." Taurat Genesis 21:1-21 NLT.

Kubadwa kwa Isake kunali chozizwa chachikuru. Momwemonso kupulumutsidwa popatsidwa kasupe wamadzi kwa Ismayeli ndi mai wake Hagara kunali chozizwa chachikuru. Kuyambira pamene Ismayeli anathamangitsidwa kunyumba kwa Abrahamu, anasamalidwa ndi Mulungu moyo wake wonse wokhala m'chipululu. "Mulungu anakhala ndi mnyamatayo…"Taurat Genesi 21:20.

Mulungu amasamala ngakhale lero. Kodi tikusalidwa? Tazingidwa ndi mabvuto osowa otithandiza? Anthu ena akutiyesa osafunika? Mulungu amamva kulira kwathu. Dzina Ismayeli limatanthauza, "Yehova amamva kusauka kwathu."

Tisamachite mantha [pamabvuto] kuti Mulungu watitaya. Iye amakhala nafe nthawi zonse monga anachitira ndi Hagara ndi Ismayeli m'chipululu nawapulumutsa kuti asafe pomwe anasowa mkate ndi madzi. Tiitanire pa Iye nthawi zonse.

## MBEU YA ISMAYELI

Patapita zaka zambiri, ndi Abrahamu ali wa zaka 175, "anamwalira, nafa m'ukalamba wake wabwino, nkhalamba ya zaka zambiri; natengedwa akhale ndi a mtundu wake." Ndipo ana ake a amuna – Ismayeli, mwana wake wamwamuna mwa Hagara, ndi Isake, anaberekera mwa Sara m'ukalamba wake—anasonkhana pamodzi, ndipo, "ana ake Isake ndi Ismayeli anamuika iye m'mphanga la Makipela, m'munda wa Efroni." Ismayeli anali wa zaka 88 zakubadwa ndipo Isake anali nazo 75.

Asanamwalire Abrahamu, anasiya phunziro lalikuru kwa anthu a lero'fe. Analimbikitsa Isake kukhalabe m'Kanani monga wolowa m'malo wake mwa lonjezano, anaonetsanso chikondi chake pa ana ake ena a amuna popatsa aliyense gawo la chuma chake. "…Koma kwa ana a akazi ake ang'ono amene Abrahamu anali nao, iye anapatsa mphatso, nawachotsa iwo kwa Isake mwana wake, akali ndi moyo, natumiza iwo chakum'mawa, **ku dziko la kum'mawa.**" Turant Genesis 25:6-9. Kuyambira pomwepo mpaka lero, ana enawo a Abrahamu akutchedwa "**anthu a maiko akum'mawa**."

Mabuku Oyera akutipatsanso "….maina a ana a Ismayeli, mwana wa Abrahamu amene mdzakazi wake (mlendo), Hagara, m' Aigupto anambalira. **Awa ndi maina a ana a amuna a Ismayeli, mndondomeko yakubadwa kwao: Nebayoti woyamba kubadwa wa Ismayeli; ndi Kedara, ndi Abideele, ndi Mibisamu, ndi Misima, ndi Duma, ndi Masa; ndi Hadada, ndi Tema, ndi Yeturi, ndi Nafisi, ndi Kedema.** Awa ndi maina a ana a amuna a Ismayeli ndipo ndiwo analinso maina a mapfuko khumi ndi awiri monga mwa midzi ndi misasa yao. Ismayeli anakhala ndi moyo zaka zana limodzi, kudza makumi atatu mphambu zisanu ndi ziwiri [137]; ndipo iye anamwalira, natengedwa akhale ndi mtundu wake," Taurat Genesis 25:12-17 TNIV. **Ndondomeko ya maina a ana a Ismayeli'yi inalembedwanso kachiwiri m'Taurat 1 Mbiri 1:28-31.**

**Mbiri, mibadwo ndi mbumba za Ismayeli sizikupezeka m'Qur'an Lolemekezeka, koma m'Mabuku Oyera a m'Malemba Oyera.** Anthu achipembedzo cha Chisalamu angathe kutsatira bwino mbiri ya chipembedzo chao'chi kuyambira pa Ismayeli. Pamene ana ake ananka akukwatirana mwa iwo okha, napanga mtundu umodzi womwe unadziwika kuti anthu amaiko akum'mawa **m'Mabuku Oyera**. Maulosi okhuza anthu akum'mawa akungopezeka m'Taurat (Chipangano Chakale) ndi Injeel (Chipangano Chatsopano/Uthenga Wabwino) mokha. Tikhala tikugwiritsa ntchito maulosi 'wa m'maphunziro a m'kabukuka.

Lero anthu a maiko a kum'mawa'wa akudziwika kwambiri m'dzina la chipembedzo cha Chisilamu. M'kabukuka tiphunzira mbiri ya anthu a maiko a kum'mawa'wa monga yalembedwera m'Bukhu Lopatulika. Mbiriyi ikuphatikiza momwe anthu'wa akhala akukhalira ndi kusakanikirana m'mabanja ndi m'mapfuko ao komanso ndi ana a Israyeli, ndiponso zomwe anachita kufikira nthawi ya Kukonzanso [Reformation] ya m'zaka za m'ma 1600. Mabuku Oyera akufotokoza kuti Mulungu, ali ndi cholingabe ndi anthuwa m'nthawi yakumapeto ino. Bukhu Lopatulika likuti iwo adzakhala m'gulu lalikuru la olungama pogwirizana ndi anthu oyera mtima a Mulungu. Tipemphere kuti kabukuka katitsegule maso, ndi kutipatsa chidziwitso changwiro kuti timtumikire Mulungu

moyenera.

## ANTHU A MAIKO A KUM'MAWA

Anthu a maiko akum'mawawa ali mbeu ya Abrahamu kudzera mwa Hagara ndi Ketura, Ketura anali mkazi wachitatu wa Abrahamu pambuyo pakumwalira Sara. Atalowera "chakum'mawa" kuchokera ku Kanani, mapfuko'wa anakwatirana nachurukana ndikudziwika ndi dzina lakuti "anthu a maiko a kum'mawa" m'Bukhu Lopatulika.

Mbiri'yi ikufotokoza kuti Mohammedi [Mneneri wa m'chipululu] anali wa pfuko la Nabayoti [Nabajioth], mwana woyamba wa Ismayeli. Ichi nchitsimikizo chakuti maina a Ismayeli ndi a ana ake ndi ofunikira kwa Mulungu. Ngati sikunali choncho, monga zikanatheka mainawo pamodzi ndi mibadwo yao kutchulidwa kawiri m'Malembo Oyera? Monga Mulungu anawatchula ndi cholinga kapena kungofuna kudzaza masamba a Mabuku Oyera ndi dzilembo za kapezi? Mulungu sanangowatchula kwachabe. Iye anali ndi cholinga ndi anthuwa. Kodi amenewa anaikidwa kumvera ndi kukwaniritsa chifuniro cha Mulungu? Ife tiyenera kumvera liu liri lonse lochokera pakamwa pa Mulungu, osawiringura.

"Mau onse a Mulungu ali angwiro…." Taurat Miyambo 30:5

## ANATCHEDWA DZOMBE

M'maulosi, a Bukhu Lopatulika "anthu a maiko a kum'mawa" amadziwikanso kuti ali "dzombe" kapena "dziwala." **Taurat Woweruza 6:1-6** Nthawi zambiri dzombe limachokera ku Arabia, pochurukitsa m'chiwerengero, mophipgiritsa, anthuwa anatchedwa dzombe.

"Ndipo ndidzakubwezerani zaka zidadya dzombe - ndi chirimamine, ndi anoni, ndi chimbalanga, **gulu langa lalikuru la nkhondo, limene ndinalitumiza pakati pa inu.**" Taurat Yoweli 2:25

"Ndipo mngelo wachisanu anaomba, ndipo ndinaona nyenyezi yochokera kumwamba inagwa padziko; ndipo anampatsa iye chifungulo cha dzenje la pompho. Ndipo anatsegula pa dzenje la pompho; ndipo unakwera utsi woturuka m'dzenjemo, ngati utsi wa ng'anjo yaikuru; ndipo dzuwa ndi thambo zinada, chifukwa cha utsiwo wa kudzenje. Ndipo m'utsimo mudaturuka dzombe padziko, ndipo analipatsa ilo mphamvu monga zinkhanira za dziko ziri ndi mphamvu. Ndipo ananena kwa ilo kuti lisaipse udzu wa padziko, kapena chabiriwiri chiri chonse, kapena mtengo uli wonse, koma anthu amene alibe chizindikilo cha Mulungu pa mphumi pao ndiwo…… Ndipo maonekedwe a dzombelo anafanana ndi akavalo okonzeka kukachita nkhondo…" Injeel Chibvumbulutso 9:1-4, 7

## LONJEZANO LA MAGAWO AWIRI LA MULUNGU KWA ANTHU AKUM'MAWA

Bukhu Lopatulika limati Hagara anali mkazi wachiwiri wa Abrahamu yemwe anambalira mwana woyamba Ismayeli. Mngelo anauza Hagara akadzichepetse kwa Sara, mkazi woyamba, amene anauza Abrahamu kuthamangitsa Hagarayo ndi mwana wake. Mulungu anakonda ndi kusamalira Hagara ndi mwana wake. Za kukwatira chiwiri Mulungu anauza Mose:

"Mwamuna akakhala nao akazi awiri, wina wokondana naye, wina wodana naye, nakambalira ana, wokondana naye, ndi wodana naye yemwe; ndipo mwana wamwamuna woyamba akakhala wa iye uja anadana naye; pamenepo kudzali, tsiku lakugawira ana ake chuma chake, sangakhoze kuyesa mwana wa wokondana naye woyamba kubadwa, wosati mwana wa wodana naye, ndiye woyamba kubadwatu. Koma azibvomereza wobadwa woyamba, mwana wa wodana naye, ndi kumwirikizira gawo lake la zake zonse; popeza iye ndiye chiyambi cha mphamvu yake; zoyenera woyamba kubadwa nzake." Taurat Deuteronomo 21:15-17 ESV

Hagara anali "wosakondedwa." Koma lonjezano la Mulungu pa mwana wake linakhala losasinthika chifukwa Ismayeli anali mwana woyamba wa Abrahamu osati Isake. Choncho Ismayeli anali " woyenera ufulu wa mwana woyamba kubadwa." **Molingana ndi lamulo'li, Ismayeli anapatsidwa magawo awiri a chuma chonse cha Abrahamu.** Lero lino zikuonekadi kuti mokhulupirika Allah anakwaniritsa pangano lake kwa Ismayeli ndi mbeu zake, powapatsa iwo moposera magawo awiri. Maiko a Kum'mawa ali ndi chuma chochuruka kotero kuti m'malo momwe munali milu ya mchenga, miyala ndi madothi, lero ndimo mukupezeka mafuta, golidi ndi chuma chambiri. Makamaka m'zaka 100 zakungothazi, Mulungu wadalitsa anthu akum'mawa ndi chuma choposa, podalitsa nthaka yao ndi powapatsa zinthu zonse zobweretsa chuma. Mulungu wasunga lonjezano lake.

**"M'malo mwa manyazi anu, owirikiza; ndi chitonzo iwo adzakondwera ndi gawo lao;** chifukwa chake iwo adzakhala nacho m'dziko mwao cholowa chowirikiza, adzakhala nacho chikondwerero chosatha." Taurat Yesaya 61:7.

Anthu a Mulungu akachititsidwa manyazi, amalonjezedwa kulandira mdalitso wopinda kawiri. Hagara amene anachititsidwa manyazi, nachotsedwa ndi kutaidwa kunja anadalitsidwa mowirikiza.

"Chifukwa chake [Sara] anati kwa Abrahamu, Chotsa mdzakazi uyo, ndi mwana wake wamwamuna; chifukwa mwana wa mdzakazi uyo sadzalowa m'nyumba pamodzi naye mwana wanga Isake." Taurat Genesis 21:10.

Yobu, m'modzi wa anthu a maiko akum'mawa, anachititsidwa manyazi chifukwa chotumikira Mulungu: kumapeto a zonse anadalitsidwa mowirikiza. "Ndipo Yehova anachotsa ukapolo wa Yobu, pamene anapempherera abwenzi ake; Yehova anachurukitsa zake zonse za Yobu mpaka kuziwirikiza." Taurat Yobu 42:10.

Mulungu akulonjeza pa Zakariya 8:7-8: "Atero Yehova wamakamu: Taonani ndidzapulumutsa anthu anga m'dziko la kum'mawa, ndi m'dziko la kumadzulo…"

**Pangano la Mulungu kwa Abrahamu likukhuza ngakhale malo a pakati pa mitsinje ikuruikuru.**

"Tsiku lomwelo Yehova anapangana chipangano ndi Abramu nati, Ndidzapatsa mbeu zako ili, kuyambira pa nyanja ya Aigupto [Nile] kufikira pa mtsinje waukuru Firate…" Taurat Genesis 15:18-21 NIV.

Dera lalikuru lonse'li ndilo Abrahamu anapatsa Ismayeli, kukhala cholowa chake pokhala iye mwana wake woyamba. Taurat Deuteronome 21:15-17. Zatsimikizikadi kuti "dera la maiko a kum'mawa" kwa Kanani lomwe Abrahamu anathamangitsirako ana ake oturuka mwa Hagara ndi Ketura ndiko kwao kwa mbeu za anawo.

Isake, mwana wa Abrahamu kudzera mwa Sara, anapatsidwa lonjezano la pangano. Za Ismayeli ndi Isake, Mulungu anati, "Koma za Ismayeli…. ndidzamyesa iye mtundu waukuru. Koma pangano langa ndidzalimbikitsa ndi Isake…. Taurat Genesis 17:20-21. Pangano ndi Isake'li linali lakuti, "mwa 'mbeu zako mitundu yonse ya dziko lapansi idzadalitsidwa." Taurat Genesis 22:18. Ndipo linalosera za **Yesu Mwana wa Mariya.**

Isake ndi mbeu zake analandira gawo lochepa chakumadzulo kwa dziko'lo. Mulungu anati, "….Ndipo ndidzakupatsa iwe ndi mbeu zako za pambuyo pako, dziko la maulendo anu, dziko lonse la Kanani likhale lako nthawi zonse; ndipo Ine ndidzakhala Mulungu wako." Taurat Genesis 17:6-8

## MAPANGANO ANAI A MULUNGU KWA ISMAYELI NDI MAI WAKE

Zokondweretsa kuti Mulungu analonjeza kumpanga Abrahamu ndi mbeu zake "mtundu waukuru." Bukhu Lopatulika likutchula "mapfuko khumi ndi awiri" a Israyeli kasanu ndi kamodzi. Awa ndi mbeu za Abrahamu kudzera mwa Isake ndi Yakobo; ndipo maina a mapfukowo alembedwanso pa zipata zolowera Kumwamba ku Yerusalemu Watsopano. Ismayeli analinso ndi ana amuna khumi ndi awiri, ndipo Mulungu anamlonjeza kuti ana ake adzakhalanso ":mtundu waukuru." Pano Aismayeli ndi mtundu waukuru kwambiri mu mbiri ya dziko.

Kwa Ismayeli ndi mai wake Hagara Mulungu anachita mapangano anai:

### PANGANO 1

"Ndipo mthenga wa Yehova anati kwa Hagara, Ndidzachurukitsa ndithu mbeu zako, kuti unyinji wao sudzawerengeka. Ndipo mthenga wa Yehova anati kwa iye, Taona, uli ndi pakati, ndipo udzabala mwana wa mwamuna; nudzamutcha dzina lake Ismayeli; chifukwa Yehova anamva kusauka



kwako." Genesis 16:10-11.

### PANGANO 2

"Koma za Ismayeli, ndamvera iwe [Abrahamu]: taona ndamdalitsa iye ndithu; adzabala akalonga khumi ndi awiri, ndipo ndidzamyesa iye mtundu waukuru." Genesis 17:20.

### PANGANO 3

Ali chilankhulire choncho ndi Abrahamu, Mulungu anati, "…uyu [Ismayeli] ndizayesa iye mtundu waukuru, chifukwa iyenso ndi mwana wako." Genesis 21:13 NLT.

### PANGANO 4

"Ndipo Mulungu anamva mau a mnyamatayo, ndi mthenga wa Mulungu anamuitana Hagara, ndi mau ochokera kumwamba, nati kwa iye, Watani, Hagara? Usaope; chifukwa Mulungu anamva mau a mnyamata kumene ali. Tauka [nyamuka], nuukitse mnyamatayo, ndi kumgwira m'dzanja lako; chifukwa ndidzampanga iye kukhala mtundu waukuru." Genesis 21:17, 18.

**CHISILAMU MU ULOSI WA BUKHU LOPATULIKA: Chibvumbulutso 9**

**Kodi Bukhu Lopatulika linaloserapo za Chisilamu? Monga Mohammed, ndi mneneri anafotokozedwa m'mabuku aulosi kuti adzachokera m'chipululu?** Mbiri ya anthu a maiko akum'mawa

ikufotokozedwa kwambiri m'Mabuku Oyera a Bukhu Lopatulika. Chisakhale chodabwitsa kuti maulosi onena za Chisilamu akupezekenso m'bukhu la Chibvumbulutso. Chibvumbulutso ndi bukhu lotsiriza m'Bukhu Lopatulika ndipo likufotokoza za zochitika za mathedwe a dziko lapansi. Kwa chifukwachi zonse ziwiri, Chisilamu ndi mneneri wochokera kuchipulululuyu, zinaloseredwa m'Chibvumbulutso mutu 9. Anthu akum'mawa akutengako gawo lalikuru m'machitachita a Mulungu mu mbiri ya mtundu wa anthu; akusewerapo gawo lalikuru m'zochitika za maora akumapeto kwa dziko ano.

Mutu 9 wa bukhu la Chibvumbulutso ukuyamba ndi chiganizo chotsirizira cha Chibvumbulutso mutu 8. Mngelo apfuula liu, "Tsoka!" katatu kwa "anthu okhala pa dziko lapansi" kuchenjeza za zomwe zichitike posachedwa.

"Ndipo ndinaona, ndipo ndinamva chiombankhanga chirikuuluka pamwamba, ndi kunena ndi mau akuru, Tsoka, tsoka, tsoka, iwo akukhala padziko chifukwa cha mau a lipenga la angelo atatu [omwe] asanaombe." Chibvumbulutso 8:13

Mau a lipenga onena tsoka katatu'wa, ndi otsiriza a mau a malipenga asanu ndi awiri. Chiwerengero cha malipenga'chi chikuimira magawidwe a nthawi yakulalikdwa kwa uthenga wabwino kuyambira pa Isa al-Masih mpaka chimaliziro cha dziko lapansi ndi yakudza kwake kwachiwiri. Chibvumbulutso mutu 9 ukufotokoza za zochitika m'nthawi yapakati pakuombedwa kwa lipenga lachisanu, ndi lachisanu ndi chimodzi monga analamulira Mulungu zomwe zinaonetsera masoka: loyamba ndi lachiwiri.

**LIPENGA LACHISANU, TSOKA LOYAMBA (Chibvumbulutso 9:1-11)**

"Ndipo mngelo wachisanu anaomba, ndipo ndinaona nyenyezi yochokera kumwamba idagwa padziko; ndipo anampatsa iye chifunguliro cha dzenje la pompho. Ndipo anatsegula pa dzenje la pompho; ndipo unakwera utsi woturuka m'dzenjemo, ngati utsi wa ng'anjo yaikuru; ndipo dzuwa ndi thambo zinada, chifukwa cha utsiwo wa kudzenje. Ndipo m'utsimo mudaturuka dzombe padziko, ndipo analipatsa ilo mphamvu monga zinkhanira za dziko ziri ndi mphamvu.

"Ndipo ananena kwa ilo kuti lisaipse udzu wa padziko, kapena chabiriwiri chiri chonse, kapena mtengo uli wonse, koma anthu amene alibe chizindikilo cha Mulungu pamphumi pao ndiwo. Ndipo analipatsa ilo mphamvu si kuti likawaphe, komatu kuti likawazunze miyezi isanu; ndipo mazunzidwe ao anali ngati mazunzidwe a chinkhanira, pamene chiluma munthu. Ndipo m'masiku ajawo, anthu adzafunafuna imfa osaipeza konse; ndipo adzakhumba kumwalira, koma imfa idzawathawa.

"**Ndipo maonekedwe a dzombelo anafanana ndi akavalo okonzeka kukachita nkhondo;** ndi pamitu pao ngati akorona onga golide, ndi pankhope pao ngati pankhope pa anthu. Ndipo anali nalo tsitsi longa la akazi, ndipo mano ao anali ngati mano a mikango. Ndipo anali nazo zikopa ngati zikopa zachitsulo; ndipo mkokomo wa mapiko ao ngati mkokomo wa agareta, a akavalo ambiri akuthamangira kunkhondo. Ndipo liri nayo michira yofanana ndi ya chinkhanira ndi mbola; ndipo m'michira mwao muli mphamvu yao yakuipsa anthu miyezi isanu.

"Ndipo linali nayo Mfumu yakulilamulira, mngelo wa pompho; dzina lake m'Chihebri Abadoni, ndi m'Chihelene ali nalo dzina Apoliyoni."

## MOMWE TSOKA LOYAMBA LIKUWAKHUZIRA ANTHU A MAIKO AKUM'MAWA

Kuombedwa kwa lipenga la 5 ndi tsoka loyamba zinayambira 622 A.D. pomwe Mohammed anathawira ku Medina…mpaka nthawi yakulandidwa kwa Constantonople pa July 27, 1449 A.D.

Tanthauzo la ulosi wa m'Chibvumbulutso 9 ndi lomveka bwino. Kwa zaka zambiri anthu owerenga Malembo Oyera, akhala akutanthauzira liu "nyenyezi" kuimira Mtumiki Mohammed monganso limaimiranso atumiki ena onse a Mulungu. Kwa Mohammed kunapatsidwa "pfungulo" lotsegulira dzenje la pompho" kapena kuti "ziphunzitso zosiyana ndi za m'Bukhu Lopatulika." Kuchokera m'dzenje la pompho'lo, munaturuka "dzombe losawerengeka. Dzombe limaimira kachurukidwe ka anthu amaiko akum'mawa. Mu mbiri ya dziko [history] anthuwa akuyerekezedwanso ndi dzombe, koma osati dzombe wamba. Dzombe'li liri akavalo okonzekera kunkhondo. Ilo linapatsidwa ulamuliro ndi Mulungu. Linasankhidwa kukhala chida cha Mulungu, chotchinjiriza anthu ake olungama komanso cholangira osalungama onse. Umu ndi momwe oipa a nthawiyo analangidwira ndi dzombelo ndi momwe olungama anatchinjirizidwira:

"Ndipo ananena kwa ilo kuti lisaipse udzu wa pa dziko, kapena chabiriwiri chiri chonse, kapena mtengo uli wonse, koma anthu amene alibe chizindikilo cha Mulungu pa mphumi pao ndiwo." Chibvumbulutso 9:4.

Mu nthawi ya Mtumiki Mohammed ndiponso pambuyo pake anthu okonda, kulemekeza, kutumikira ndi kuchita chifuniro cha Mulungu m'chachoonadi anatchedwa "Anthu a Bukhu." Anthu olungama ndi gulu lomwe "dzombe-akavalo" linauzidwa kuti **lisawaononge**. Abubeker yemwe analowa m'malo mwa Mtumiki Mohammed, polangiza atsogoleri a gulu lake la nkhondo, anakwaniritsa mau a m'Bukhu Lopatulikawa motere:

"Pambuyo Mohammet [Mohammed} atamwalira, Abubeker analowa m'malo mwake kukhala mtsogoleri m' A.D. 632: ndipo atakhazikika pa utsogoleri wake kwa kanthawi, iye analemba ndi **kutumiza makalata kuzungulira mapfuko onse a m'Arabia**, nati:

"'Ndikufuna kukudziwitsani kuti ndaganiza zotumiza ankhondo a m'chipembedzo ndi chikhulupiriro chathu ku Syria kuti akalande dzikolo m'dzanja la anthu onyoza Mulungu, ndikufunanso muzindikire kuti nkhondo ili yonse yochitika m'dzina la chipembedzo ili chizindikilo chakuchita chifuniro cha Mulungu ndi chakumvera Iye.'

"Amithengawo atapita, anabwerera ndi yankho lolimbikitsa za nkhondoyo, kuchokera ku zigawo zonse: ndipo mosakhalitsa malo a ankhondo ku Medina anadzadza ndi magulu a amuna olimba mtima ndi opanda mantha a chi-Saracen, omwe anafunitsitsa kuchitapo kanthu pa zomwe mtsogoleri wao anawauza, ngakhale ankhondowo anadandaula za nyengo, komanso kusowa kwa zofunikira zambiri pa nkhondoyo, ndiponso m'chitidwe wong'ung'uzang'ung'uza pakati pao, ndi kuchedwetsa zinthu komwe Abubeker anakuchita. Chiwerengero chao chitakwanira, Abubeker anakwera pa phiri, nayang'ana pa amuna anasonkhanawo, akavalo ndi zida, napemphera iye pemphero lodzikhuthula ndi losweka mtima, lofunira mafuno abwino gulu la nkhondolo. Kwa atsogoleri a ku Syria, iye anawalimbitsa mtima, powatumizira uthenga owatsimikizira za chipambano ngakhale nkhondoyo inali isanachitike, ndipo iye anangochita ichi mwa umunthu.

Wotsatira Mtumwi Mohammed'yu analangiza gulu lopita kunkhondolo: "'Musayiwale ichi,' anatero iye, 'muli pamaso pa Mulungu ndipo Iye akukuonani nthawi zonse, kaya moyo wanu ukakhala pa chiopsezo cha imfa, muzindikire kuti mudzaweruzidwa, choncho khalani ndi chiyembekezo chodzalowa m'Paradiso: kapeweni chisalungamo china chiri chonse kuphatikiza kupondereza ena; kambiranani wina ndi mnzake mukasemphana, ndi kumvetsetsana pofuna kukweza chikondi ndi umodzi wa gulu lanu. Pamene mukukamenya nkhondo ya Ambuye, kaonetseni chamuna, kapiteni chitsogolo nthawi zonse osayang'ana m'mbuyo; **chipambano chanu chisakadetsedwe ndi mwazi wa akazi kapena ana. Musaononge mitengo ya kanjeza, kapena kuotcha minda ya tirigu ndi moto. Musakalikhhire pansi mitengo ya zipatso,** kapena kuchitira choipa chiri chonse ziweto; kupatula kupha zokhazo mufuna mudye. Mukapangana pangano liri lonse, khazikikani mu limenelo osaliswa, onetsani ubwino wanu m'mau ndi mu ntchito zanu zabwino. **Mukapeza anthu opembedza ali m'malo ao opembedzeramo, nimtsimikiza kuti akutumikira Mulungu m'choonadi kawasiyeni osawapha, musaononge malo ao:** koma mukapeza gulu l**a sunagoge wa Satana atabvala tidzipewa tao:** musakawasiye ndi m'modzi yemwe, mukabvule tidzipewato ku mitu yao, ndikuwakakamiza alowe Chisilamu ndipo akakana muwalipiritse ndalama zochuruka.'" Josia Litch, *Prophetic Exposions,* Vol. 2, 1842, p. 172-3.

**Mulungu anaika mzimu wa chifundo mwa a Saracen, wochitira ulemu akhristu onse olungama omwe amakhala m'madera a okhaokha, ndi kusunga malamulo ake:** koma kwa ansembe a chi-Roma ndi anthu omwe amakhala nao m'malo a mtundu womwewo, ndipo samasunga malamulo a Mulungu zinthu sizinali choncho. Anaphedwa, kupatula ngati atabvomera kulowa Chisilamu kapena kulipira ndalama. M'kanthawi kochepa Syria yense analandidwa ndi a Saracen." Steven Haskell, *Seer of Patmos*, 1903, p. 167.

Chipembedzo cha Chisilamu chimalekanitsa pakati pa magulu osiyana a Chikhristu, tsimikizirani powerenga m'Qur'an Lolemekezeka:

**"Ndi osiyana: Anthu a Bukhu [Akhristu olungama] ndi kagulu kochepa koma koima (pa choonadi); Iwo amachita Zizindikiritso za Mulungu usiku wonse, naweremitsa nkhope zao pansi kumlambira mompatsa ulemu.** Amakhulupirira mwa Mulungu ndi Tsiku Lachimariziro; amakondwera ndi choonadi ndi chilungamo ndi kudana ndi chosalungama chiri chonse; ndipo (amadziwika) ndi ntchito (zonse) zabwino: **Iwo ali kagulu kokhako kosakhala m'mabwalo a onyoza."** Sura 3:113-114 Al-E-Imram

Qur'an Lolemekezeka likuchitira umboni kuti si onse omwe amadzitcha akhristu ali akhristu oona. Likufotokoza kuti akhristu enieni, ndi anthu omwe akuchita zizindikiritso za Mulungu, olekanitsa chabwino ndi choipa, ndikukhala mgulu la "olungama!" "Chizindikiritso" chimodzi, chomwe akhristu enieni ayenera "kumachikumbukira" ndi kuchichita: Ndi kulilemekeza Sabata (Sabat) Loyera lakupumula la tsiku lachisanu ndi chiwiri, Saturday monga mwa lamulo la Mulungu.

"Mudzisunga masabata anga ndithu: pakuti ndiwo chizindikilo pakati pa Ine ndi inu mwa mibadwo yanu; kuti mudziwe kuti Ine ndine Yehova wakukupatulani." Eks. 31:13

Kuchokeranso m'Qur'an kwalembedwanso,

Mkati mwa anthu odzitchawo akhristu, "Ndi iwo, iwonso, akudzitcha akhristu, tinachita nao pangano, koma iwo ananyalanyaza mbali yaikuru ya Uthenga womwe unapatsidwa kwa iwo… Ndipo posachedwa Mulungu awazindikiritsa iwo za chosalungama akhala akuchichitacho." Sura 5:14 Al'Maeda.

Za ulosi wa lipenga lachisanu ndi tsoka loyamba, Asaracen ndi umodzi wa mitundu ya anthu amaiko akum'mawa omwe anakwaniritsa Chibvumbulutso 9. Mbiri ya dziko ikuchitiranso umboni kuti panakhala "kuzunzidwa" kwa anthu mu Ufumu wa Aroma Wakum'mawa, monga momwe linanenera Bukhu Lopatulika. Ankhondo a chi-Saracen anathira nkhondo Ufumu wa Aroma Wakum'mawa kwa miyezi isanu, **ndendende** nthawi yomwe inatchulidwa m'mau aulosiwu kuti kudzatero.

"Ndipo [dzombelo] liri nayo michira yofanana ndi ya chinkhanira ndi mbola; ndipo m'michira mwao muli mphamvu yao yakuipsa anthu miyezi isanu." Chibv. 9:10.

Masiku a miyezi isanu ya ulosiwu ndi 150 kuimira zaka 150. M'ulosi, tsiku limodzi limaimira chaka chimodzi. M''kawerengedwe ka chi-Hebri mwezi uliwonse uli ndi masiku 30, ndipo chaka chiri ndi masiku 360.

"….tsiku limodzi kuwerenga chaka chimodzi…." Taurat Numeri 14:34.

Asaracen pansi pa Ottman, anayamba "nkhondo" yao ya miyezi isanu, nalowa Ottoman mu Ufumu wa Aroma Wakum'mawa pa July 27, 1299. Pa nthawiyi iwo sanatumidwa kuuthetseratu Ufumuwo, koma kungouzunza kwa zaka 150.

"Ndipo [dzombelo] linali nayo Mfumu yolilamulira, mngelo wa phompho; dzina lake m'Chihebri Abadoni, ndi m'Chihelene ali nalo dzina Apoliyoni." Chibv. 9:11

Maina onse awiriwa akutanthauza "woononga." Ulosiwu ukuonetsa kuti poyamba "dzombe" linatumizidwa "kukangozunza," koma m'tsoka lachiwiri, linatumidwa kukaononga. Mbiri ikutsimikizira za zomwe gulu liri lonse linakaichita.

**Chibvumbulutso 9:1-11 Kufalikira kwa Chisilamu.**

Kwa zaka pafupifupi 600 chiwerengero cha Aluya chinali ngati dzombe koma lopanda mfumu. Kumapeto kwa zaka za m'ma 1200, Ottman anakhazikitsa boma. Pa July 27, 1299 analowa m'Nicomedia – kuchita nkhondo yake yoyamba ndi Ufunu Wakum'mawa wa Aroma. Anapatsidwa mphamvu yakuzunza anthu kwa miyezi isanu, kuimira zaka 150. Ichi chinachitika kuyambira July 27, 1299 mpaka July 27, 1449 nthawi yomwe ikupezeka pophatikiza July 27, 1299 ndi 150." Steven Haskell, *Bible Handbook for Students of Prophecy*, 1919, p. 121.

## LIPEMGA LACHISANU NDI CHIMODZI: TSOKA LACHIWIRI

"Tsoka loyamba lapita; taonani akudzanso masoka awiri m'tsogolomo.

"Ndipo mngelo wachisanu ndi chimodzi anaomba, ndipo ndinamva mau ochokera ku nyanga za guwa la nsembe lagolide liri pamaso pa Mulungu, nanena kwa mngelo wachisanu ndi chimodzi wakukhala ndi lipenga, Masula angelo anai omangidwa pa mtsinje waukuru Firate. Ndipo anamasulidwa angelo anai, okonzeka kufikira ora ndi tsiku ndi mwezi ndi chaka, kuti akaphe limodzi la magawo atatu a anthu [tsoka lachiwiri]. Ndipo chiwerengero cha ankhondo apakavalo ndicho zikwi makumi awiri zochurukitsa zikwi khumi; ndinamva chiwerengero chao.

"Ndipo kotero ndinaona akavalo m'masomphenya, ndi iwo akuwakwera akukhala nazo zikopa za moto, ndi huakinto ndi sulfure; ndi mitu ya akavalo ngati mitu ya mikango; ndipo m'kamwa mwao munaturuka moto ndi utsi ndi sulfure. Ndi miliri iyi linaphedwa limodzi la magawo atatu a anthu, ndi moto, ndi utsi, ndi sulfure, zoturuka m'kamwa mwao. Pakuti mphamvu ya akavalo iri mkamwa mwao, ndi m'michira yao; pakuti michira yao ifanana ndi njoka, nikhala nayo mitu, ndipo aipsa nayo.

"Ndipo otsala a anthu osaphedwa nayo miliri iyo sanalapa ntchito ya manja ao, kuti asapembedzere ziwanda, ndi mafano a golide, ndi siliva, ndi a mkuwa, ndi amwala ndi amtengo, amene sakhoza kupenya, kapena kumva, kapena kuyenda; ndipo sanalapa mbanda zao, kapena nyanga zao, kapena chigololo chao kapena umbala wao." Chibv. 9:12-21.

## TSOKA LACHIWIRI NDI CHISILAMU

Kunena kuti mauthenga onena za chilango a m'Chibvumblutso 9 amachokera kwa Mulungu munthu sangatsutse chifukwa cha mau a lipenga la 6 ndi tsoka lotsatizana. Bukhu Lopatulika likuti, mau otuma dzombelo anachokera "ku nyanga za guwa la nsembe la golide liri pamaso pa Mulungu m'Kachisi wakumwamba." **Mau'wa akutsimikizira kuti Mulungu analora zinachita Asilamu'wo.**

Nanga ndi pandani anati tsokali ligwere? Molingana ndi lipenga la 6 – tsokali linaperekedwa kugwera pa chipembedzo cha mafano; pa yense anamva **chidzudzulo cha Mulungu** koma "wosalapa"--- ligwere pa mchitidwe wa chipembedzo chonyoza Mulungu chomwe chikhazikitsidwe kumatsiriziro adziko lapansi chofanana ndi cha Upapa chomwe chinachitikapo; ligwere pa **upapa wa Aroma komanso onse olumikizana nao**. Ulosi wa m'Chibvumbulutsowu kutiuzanso kuti chipembedzo chabodzachi chidzachita mgwirizano ndi mipingo ya Mipanduko [Protestants] yakugwa (mneneri wonyenga) ya dziko la America koma chipembedzocho chidzalangidwa ndi miliri ya mkwiyo wa Mulungu. Ndipo kumapeto chirombocho ndi mneneri wonyengayo adzaponyedwa m'nyanja yamoto yotentha ndi sulfure:

"Ndipo chinagwidwa chirombocho, ndi pamodzi nacho mneneri wonyenga amene anachita zizindikilo pamaso pake, zimene anasokeretsa nazo iwo amene adalandira lemba la chirombo, ndi iwo akulambira fano lake; iwo awiri anaponyedwa ali moyo m'nyanja yamoto yakutentha ndi sulfure." Chibvumbulutso 19:20.

**Mulungu anagwiritsa ntchito ayani kukwaniritsa tsoka lachiwiri? M'nthawi ya Kukonzanso [Reformation] Mulungu akugwiritsanso ayaninso?** "Ndipo mngelo wachisanu ndi chimodzi anaomba, ndipo ndinamva mau ochokera ku nyanga za guwa la nsembe lagolide liri pamaso pa Mulungu, nanena kwa mngelo wachisanu ndi chimodzi wakukhala ndi lipenga, Masula angelo anai omangidwa pa mtsinje waukuru Firate. Ndipo anamasulidwa angelo anai okonzeka kufikira ora ndi tsiku ndi mwezi ndi chaka, kuti akaphe limodzi la magawo atatu a anthu." Chibvumbulutso 9:13-15

Angelo anai omangidwa ku mtsinje wakuru Firate ndipo anasulidwa chifukwa nthawi ya utumiki wao inakwana, anali mafumu [a Sultan] akuruakuru anai a Chiluya – Bagdad, Damascus, Iconium ndi Aleppo – omwe anachita mgwirizano wamphamvu wa ulamuliro wa Chisilamu. **Mau akuti mafumuwo amasulidwe, akutanthauza, kuti Mulungu anapatsa otsatira Mohammed'wa mphamvu zochita nkhondo, kuononga, kuchotsa ndi kufafaniziratu Ufumu [Wakum'mawa] wa Aroma.** A.T. Jones, *Great nations of Today*, 1902, p.73

**"Ora, ndi tsiku, ndi mwezi, ndi chaka,"** zoperekedwa kuti "akaphe limodzi la magawo atatu a anthu" (Chibvumbulutso 9:15) zikuimira nthawi ya lipenga la tsoka lachiwiri. Kawerengedwe ka nthawi kameneka kakuti "ora limodzi, tsiku ndi mwezi ndi chaka" kamagwiritsanso ntchito katanthauzidwe kakuti (mu ulosi "tsiku limodzi " limaira chaka chimodzi), choncho zonse zatchulidwa pamwambazi zikupanga zaka 391 ndi masiku 15 motere:

Ora = gawo la maora 24 la tsiku lonse kuimira masiku 15



Tsiku = chaka 1


Mwezi = masiku/zaka 30

Chaka = masiku/zaka 360

Kuphatikiza zonse = 391 (masiku/zaka) ndi masiku 15

Tsoka lachiwiri la kuomba kwa lipenga lachisanu ndi chimodzi linayambira pomwe panathera lipenga lachisanu ndi tsoka loyamba pa July 27, 1449 kufikira pomwe panathera ufumu wa chi-Turk wa Ottman pa August 11, 1840. Pa tsiku lomwe nthawi ya chaka, mwezi, tsiku ndi ora zinathera ufumu wa Othman unagonja ku maufumu anai a ku Ulaya. Ufumu wa Ottman unatha ndendende nthawi ya zaka 391 ndi masiku 15.

“… Mafumu ( a Sultan) anaiwa Aleppo, Iconium, Dmascus ndi Bagdad anali maziko olimba a Ufumu wa




Ottman…Koma mphamvu ya Ufumu'wu inaneneredwa kuti idzatha m'ora, tsiku, mwezi ndi chaka, kutanthauza nthawi yotalika zaka 391 masiku 15. Ufumu'wu unapatsidwa kukhala wamphamvu, kuyambira pa July 27, 1449 + zaka 391 masiku 15 ndipo unatha pa Agust 11, 1840.” Steven Haskel, *Bible handbook for Prophecy*, 1919, p121.

Chisilamu kudzera mwa **anthu a chi-Turk pansi pa Ottman, chinali chida chimene Mulungu anachigwiritsa ntchito kukwanitsira ulosi wa Bukhu Lopatulika.** Anthu amaiko akum'mawa'wa anapatsidwa ulamuliro kuchokera pa nyanga za guwa la golide lomwe liri pamaso pa Mulungu “kupha” gawo limodzi la magawo atatu a Ufumu wa Aroma lomwe linali ufumu wa “Ahelene” womwe likuru lake linali Constantinople.

“Pamene mngelo wachisanu ndi chimodzi anaomba, kunalamulidwa kuti zichotsedwe zokhumudwitsa zonse zomwe zinaikidwa kuupinga mtunduwo [Turkey Ottman], … ndipo ulamuliro wao unakuzidwa ndi kukhala ndi mphamvu yakupha gawo limodzi la magawo atatu la anthu…..” Uriah Smith, *Daniel and Revelation,* 1897, ndemanga ya Chibvumbulutso 9:15. Asilamu'wa anakwaniritsadi ulosiwu, ndipo mzinda wa Constantinople unagwadi m'dzanja lao. Ufumu Wakum'mawa wa Aroma unathera pomwepo. Dzina lalikuru lake Constantinople linasinthidwa mzindawo nudziwika kuti Istanbul, Turkey.

M'chaka cha 1840 panajambulidwa ndondomeko m'zithunzi yoonetsa kuti Asilamu analidi Angelo Okhantha omwe anagwiritsidwa ntchito kukwaniritsa ulosi wa Bukhu Lopatulika wa Chibvumbulutso 9.

Ichi chititsimikizire ife kuti pangatenge nthawi yotalika bwanji maulosi a Mulungu amakwanitsidwa..

## KUKONZANSO KWA AMPANDUKO [PROTESTANTS] NDI CHISILAMU M'ZAKA ZA M'MA 1500

Ndi m'nthawi ya kuomba kwa lipenga la chisanu ndi chimodzi pomwe Kukonzanso [Reformation] kwa m'zaka za 1500 kunayamba ku maiko a ku Ulaya. Anthu ena mu mpingo wakugwa wa Aroma anaturukira zolakwika zake naupandukira. Wotsogolera wao anali mbusa watchuka uja wa ku Wittenberg, Germany – Martin Luther.

Chinthunzi ichi chinajambulidwa 1850 kufotokoza kudzera m'zithunzi za matsoka 1 ndi 2 otsatira kuombedwa kwa malipenga a m'Chibvumbulutso 9 kuti amatanthauza kugwiritsidwa ntchito ndi Mulungu kwa Chisilamu. Kuyambira m'mbuyomu kufikira lero a mipingo ya Mpanduka [Protestants] akhala akubvomereza katanthauzidwe ka Chibvumbulutso 9'ka.

Ndi m'nthawi yakuomba kwa lipenga lachisanu ndi chimodzi momwe **Chisilamu chinatumikira Mulungu potchinjiriza anthu ake olungama omwe ufumu wachitsulo ndi wankhanza wa Mpingo wa Aroma unafuna kuwaononga**. Alembi a Mbiri ya dziko afotokoza zabwino zambiri zomwe Chisilamu chinazichita mu nthawi Kukonzanso ya a Mpanduko [Protestant Reformation]. M'munsimu zalembedwa zina za zomwe Chisilamu chinachita potumidwa ndi Mulungu Wam'mwambamwamba. Ndipo zikuonetsera mgwirizano womwe unalipo pakati pa Asilamu ndi “Israyeli Wauzimu” yemwe anali a Mpanduko aku Ulaya.

“Asia linali pansi pa ulamuliro wa Soliman Wopambana [the Magnificent]. Nthawi zonse magulu ake ankhondo anaonekera akuthamangathamanga, ngati kung'anima kwa mphenzi, m'malire ndi maiko a Chikhristu. Pakadzuka mtopola wozunza a Mpanduko Okonzanso, ndipo maufumu amene amagwirizana ndi ulamuliro wa m'Episikopi wa Aroma [Upapa] akalumikizana kuti aononge anthu a Mulungu ndi lupanga, komanso kuwaopseza kuti achite mantha, Asilamu momvera ndi kuchita chifuniro cha Mulungu yemwe sanamzindikira, anatchinga malire onse a Ulaya Wakum'mawa mu mphamvu yosaimvetsetsa munthu, kotero kuti malupanga amene anakonzedwa kuphera a Mpanduko osowa wowatchinjirizawo anaonongedwa osawafikira iwo. Anthu a mtundu wa chi-Turk'wa anali ndodo yong'anima ngati ukali wa mphenzi yomwe inaziziritsa namondwe. <u>Khristu anatchinjirizira nkhosa zake zochepazo pogwiritsa ntchito Chisilamu kukhala tchinga lao</u>.” J. A. Wylie, *History of Protestantism*, Volume 1, p.474.

“Litayenda kuchokera malire ena, kudutsa m'dziko'lo kufika ku malire ake ena a dziko la Hungary, khamu lankhondo la Ottman, linafika nilikhala pansi pafupi ndi malinga a Vienna mulungu umodzi Msonkhano Waukuru wa Marburg usanachitike. Mapiri ozungulira likuru'lo anaoneka kuti mbuu ndi misasa yao, ndipo zigwa za chonde zinali m'munsi mwa malingawo, zomwe ndi kale lonse sizinapondedwepo ndi akavalo a chi-Mussulman, zinatsenderedwa pansi ndi khamu lalikuru la akavalo. Asilikariwo anakumba maenje akuya, nkumaomba mfuti zao, kwinaku ataboola kale linga la mzindawo. Panangokhala masiku ochepetsetsa kuti Vienna agwe m'manja mwa khamu, la mphamvu, ndi lolimba ku nkhondo la Ottman, ndiponso kuti chionongeko ndi mwazi-ngati madzi mu mtsinje zikhale mbiri yosaiwalika.

“Chipata cha Germany chinaphwasulidwa osatsekekanso, ogonjetsawo analowa mwamkokomo ngati madzi osefukira m'khwalalala la Danube, ndi m'khalango za mitengo, kudutsa mizinda ndi madera ophwasuka a Ufumu'wo. Chinalikudzacho chinali choopsa ndithu. Chionongeko cha onse chinayandikira ngati mkokomo wa madzi osung'unuka omwe anaundana pa nsonga za mapiri a Alp, ichi chinadetsa nkhawa magulu ndiponso atsogoleri m'Germany, kuti chidzagwera pa iwo ndi phwasulo lalikuru. 'Ndinu' anatero iwo okhulupirira ziphunzitso za upapa kuwanamizira a Luthren, 'mwapangitsa kuti chilango [cha a Turk] chitigwere. Ndinu amene mwachititsa kuti angelo akuphawa amasulidwe: kudzakulangani chifukwa chakuukira Mulungu kwanu. Mwakana kukhala pansi pa ulamuliro wa Papa, ndiye tsopano mukhaule pokhala m'ukapolo wa a Turk.

“'**Si zimenezo ai,' anayankha Luther, 'Ndi Mulungu amene walimasula gulu la nkhondo'li, lomwe mtsogoleri wake ndi Abadoni woononga.** Iwo atumizidwa kudzationonga chifukwa cha machimo athu, kusasamala uthenga wabwino kwathu, kuchitira mwano dzina la Mulungu, ndiponso kukhetsa mwazi wa olungama kwathu.'” Ibid., p.597.

“**A Turk anali ndodo-m'dzanja la Mulungu yolangira oipa ndi yozimitsira kung'anima ngati kwa mphenzi kwa upandu wa Vatican, nakhala iwo tchinga la olungama ku Ulaya.**” Ibid., Volume 2, p.598.

“**A Turk anadzipereka mosazengereza kukapulumutsa Hungary wa Mpatuko,** koma sanazindikire kuti anatumidwa ndi Mulungu. Soliman Wopambana [the Magnificent], ananyamuka ku Constantinople pa 23rd April, 1526, natsogolera gulu lalikuru la nkhondo, lomwe, posapezana ndi choletsa chiri chonse linanka likuonjezeka kufika pa 300,000, ndipo linayandikira Hangury ndi kuopsya ngati 'ukali wa bingu.'

“Dziko linanjenjemera niligwidwa mantha akuru, Mfumu Louis analibe ndalama ndiponso asilikari okwanira. Atsogoleri othandizana naye anagawikana m'timagulu: ansembe anatangwanika kulimbana ndi anthu a Mpanduko; anthu wamba, popsinjidwa ndi malamulo a ansembewo ndi kukanizidwa ufulu wao, analibe chidwi kapena kukhuzidwa. Zapolya, mtsogoleri wa mizinda makumi asanu ndi awiri mphambu awiri [72], ndiponso wamphamvu ndi gogo wodziwika m'dzikomo, sanatekeseke, koma kudikira ufumu wa Aroma ugwe kuti iye akhazikitse wake.

“A Turk'wo anayandikira, natumiza amithenga akuti Louis adzipulumutse powapatsa ndalama zochuruka, ndi kuti ngati iye satero aukiridwa ndi mipingo yonse ya m'Hangury, ndi kumpha pamodzi ndi zidzukulu zake ngati 'ng'ombe zonenepa.

“Lamulo lakuti a Mpanduko aphedwe silinanthidwe, ndipo **amuna odzipereka kugwira ntchito osalipidwa a mpingo wa Aroma [monks], mosasamala za mtambo wa namondwe wa chionongeko chinali kuchokera kum'mawa, analimbikirabe kudzutsa mkwiyo wa anthu pakunenabe kuti onse otsatira Luther aphedwe.**

“…Mfumu Louis anakatchinga Soliman ku njira. Pa 29th August asilikari ake 27,000 analimbana ndi chikhamu cha nkhondo cha Turkey ku Mohacz, pa Danube. Chiwerengero cha ankhondo a Soliman chinapinda kakhumi ndi kasanu cha gulu la Louis. Louis anapatsa ulamuliro wa gulu lake kwa m'Episikopi wamkuru wa Cologne – yemwe anakhalapo m'chipani cha Francis Woyera m'mpingo wa Aroma, katswiri pa nkhondo yalupanga, wotchukanso m'zachikunja kuposa za m'kachisi.

“Pamene mfumu inabvala za nkhondo zake m'mawa womwe imapita kunkhondo, nkhope yake inaoneka ya nkhawa ndi yotumbuluka. Anthu onse anachiona ichi. 'Pano akunyamuka amuna a chi-Hungary zikwi makumi awiri ndi zisanu mphambu ziwiri!'

Anapfuula Episkopi Pereyi pamene ankhondowo amadutsa…Koma pofika madzulo a tsiku'lo chigwa cha Mohacz chinadzaza ndi mitembo yosamba magazi ya a Hungary. Mitembo ya akalonga makumi awiri ndi asanu ndi atatu, mfulu mazana asanu, a episkopi asanu ndi awiri, kudzanso asilikari a nkhondo zikwi makumi awiri inagona pansi osati nkuukanso. Pothawa kuchokera ku malo a imfawo, mfumu pamodzi ndi nthumwi ya papa anafuna malo oti abisareko. Louis anaoloka dziwe lakuda linali pafupi naye; kavalo yemwe anamuolotsa dziwelo, polephera kukwera chitunda cha tsidya linalo, anagwa chambuyo ndi kumupha iye, ndi kupanga zithaphwi momwe munamera mantcheza kukhala manda ake. Nthumwi ya papa, yoonekayo ngati mneneri wotsika mapiri a Aram, inagwidwa ndi kuphedwa. Atatha kugonjetsa mfumu Louis ndi gulu la nkhondo lake, Soliman wolakikayo analowa m'Hungary, naphamo anthu 200,000. "**Choopsya chachikuru ichi, chinagwedeza Ulaya yense, ngakhale kwinaku chinapatsa mpumulo kwa akhristu a Mpanduko.**" Ibid., Vol. 3, p. 221.

## LIPENGA LOTSIRIZA LA CHI - 7: TSOKA LACHITATU

Kuyambira October 22, 1844 lipenga lotsiriza la malipenga asanu ndi awiri la Chibvumbulutso 8, 9, ndi 10 lakhala likuombedwa pa dziko lapansi. Tiri m'tsoka lachitatu ndi lotsiriza – la lipenga la chi – 7 ndi lotsiriza la m'Cnibvumbulutso:

"Komatu m'masiku a mau a mngelo wachisanu ndi chiwiri m'mene iye adzayamba kuomba, pamenepo padzatsirizika chinsinsi cha Mulungu, monga analalikira kwa akapolo ake aneneri." Chibvumbulutso 10:7

Pamene tirinso ku matsiriziro a mbiri ya dziko, Chisilamu chikunka chikukhalanso cha mphamvu kwambiri m'dziko lapansi. Ntchito ya "dzombe" m'tsoka lachitatu lomwenso ndi lotsiriza idzakhalanso ngati yomwe Asilamuwa anaichita m'matsoka awiri a malipenga oyamba aja. Taphunzira kuti "angelo anai" omwe anamasulidwa m'tsoka lachiwiri "anakonzetsedwa za ntchito anaichitayo – anasankhidwa, naphunzitsidwa ndi dzanja losaoneka [la Mulungu] kukachita ntchito anaitanidwirayo. Za ankhondo a chi-Turk, zikuoneka kuti, chikonzetsero chao, chinadalira pakukulirakulira mphamvu ndi kugwirizanika kwao pamodzi…" *Barnes' Commentary on Revelation*, p. 264, in Walter E. Straw, *Studies in Revelation,* 67-8

**Kodi mtsogolomu "dzombe" lidzaononganso moonjeza?** Cholinga chenicheni cha dzombe chinali kuti likaononge anthu onse opotoza Mau a choonadi, koma nkumadzitcha atumiki a Mulungu – iwo amene anagwirizana ndi upapa wa Aroma.

**Monga udzatsanulidwa mkwiyo wa chiweruzo wa Mulungu pa otero'wo?** M'lipenga lotsiriza'li, chiweruzo chikuchitika m'mwamba, ndipo pamene chitsirizika, chitetezero cha amitundu chitsekedwa. Pomwepo Isa Mwana wa Mariya, aonekera akutsika kudzadzutsa olungama ndi kutenga pamodzi nao olungama amoyo kunka nao kumwamba.

Ino ndi nthawi yakuti amitundu modzichepetsa adze kwa Mulungu, ndi Malamulo ake Oyera, ndi kwa Mwana wa Mariya, amene anatumizidwa pansi pano kudzakhala nsembe ya machimo athu. Isa [Yesu] ali bvumbulutso la chifundo cha Mulungu. Mwa Yesu Mwana wa Mariya chilungamo cha Mulungu chimapatsidwa kwa ife. Si kwa ife tokha, koma kwa anthu onse amene amlandira Yesu ndi mphamvu yake yakupulumutsa; Iye amene njira zake zimatitsogolera kukusunga malamulo Oyera a Mulungu.

## KUDZIPEREKA KWATUNTHU KWA MULUNGU: YESAYA 60

Munthu ndani angadzipereke kotheratu kwa Mulungu ndiponso ku mauthenga a choonadi chake? Yesu anati Iye ndiye Mbusa wa nkhosa, kutanthauza kuti ndi Iye amene anatumidwa kudzatsogolera anthu a Mulungu pa dziko lapansi pano. Za Ubusa wa Isa, Daudi [Davide] m' Zabur anati,,

"Yehova ndiye mbusa…." Zaburi Masalmo 23:1. Isa anati, "Ine ndine Mbusa Wabwino; mbusa wabwino ataya moyo wake chifukwa cha nkhosa." Injeel Yohane 10:11

Yesu anatinso: "Ndipo nkhosa zina ndiri nazo, zimene siziri za khola ili; izinso ndiyenera kuzitenga, ndipo zidzamva mau anga; ndipo zidzakhala gulu limodzi, mbusa mmodzi." Injeel Yohane 10:16

Funso: **Kodi "nkhosa zina" anazinena Yesu kuti afuna atazibweretsanso m'khola lake ndi ziti?** Zolembera za m'modzi wa aneneri akale zikuyankha:

"Gulu la ngamila lidzakukuta, ngamila zazing'ono za Midyani ndi Efa; iwo onsewo adzachokera ku Seba adzabwera nazo golide ndi zonunkhira; ndipo adzalalikira matamando a Yehova. Zoweta za Kedara zidzasonkhana kwa iwe, nkhosa za mphongo za Nebayoti zidzakutumikira; izo zidzafika ndi kulandiridwa pa guwa langa la nsembe; ndipo ndidzakometsa nyumba yanga ya ulemelero wanga." Taurat Yesaya 60:6-7.

"Ndipo maina a ana a Ismayeli ndi **Nebayoti**; ndi **Kedara**, ndi Abideeke, ndi Mibisamu mdi Misima, ndi **Duma**, ndi Masa, ndi Hadada, ndi Tema. Ndi Yeturi ndi Nafisi ndi Kedama: Awa ndi maina a ana a Ismayeli…." Taurat Genesis 25:13-16.

"Ndipo Abrahamu anatenga mkazi wina dzina lake Ketura. Ndipo anambalira iye Zimerani ndi Yokesani ndi Medani, ndi **Midyani**, ndi Yisebati, ndi Sua. Ndipo Yokesani anabala Seba, ndi Dedani. Ana a Dedani ndi Aasuri, ndi Aletusi ndi Aleumi. Ana a Midyani: **Efa**, ndi Efere, ndi Hanoki, ndi Abida, ndi Elida…." Taurat Genesis 25:1-6.

Abrahamu anachotsa ana ake awa ku Kanani kukakhala kum'mawa. Iwo anasakanikirana ndi kukwatirana pakati pao, natchedwa, "anthu a maiko akum'mawa." Mwachitsanzo, Esau mwana wa Isake, anakwatira mwana wa mkazi wa Ismayeli.

"….ndipo ananka [Esau] kwa Ismayeli, naonjezera kwa akazi amene anali nao, natenga Mahalati mwana wamkazi wa Ismayeli mwana wa Abrahamu, mlongo wake wa Nebayoti akhale mkazi wake." Taurat Genesis 28:8-9

Choncho mau a pa Yesaya 60:6-7 ali ulosi wonena za nthawi yakumapeto a dziko lapansi pomwe anthu a maiko akum'mawa'wa adzakhala amodzi a anthu oopa ndi kutumikira Mulungu moona mtima. Ana a **Nebayoti**, **Kedara**, **Sheba**, **Midyani**, **Efa**, **Duma**, [a Chisilamu] atchulidwa mwachindunji. A**nthu a maiko akum'mawa adzatengapo gawo lalikuru pakulumikizana ndi "anthu a Bukhu" [akhristu olungama] a Mulungu, kukanitsitsa kunyoza ndi kupondereza choonadi cha Bukhu Lopatulika, iwo adzakanitsitsa kusintha nao mau ndi malamulo a Mulungu.** Anthu a Bukhu ndi Asilamu mogwirizana adzachita choonadi limodzi.

**Monga Asilamu olungama adzawazindikira "akhristu oona" ndi odalitsika a Mulungu?** Mlembi wa kabukuka akukhulupirira kuti anthu eni Bukhu ndi a Seventh – day Adventist olungama. Tapezanani ndi m'modzi wa iwo…Mosakaika konse anthu amaiko akumm'mawa ku nthawi yakumapeto ino adzati kwa "anthu a Bukhuwo:" **"Kuona tinaona kuti Yehova ali ndi iwe: ndipo tinati, Tilumbiriranetu tonse awiri ife ndi iwe…"** Taurat Genesis 26:28 NIV

## NKHAWA YA DUMA

"Nkhawa ya Duma: Wina aitana kwa ine kuchokera ku Seiri, Mlonda, nthawi yanji ya usiku Mlonda, nthawi yanji ya usiku? Mlonda anati, Kuli kucha, koma kukali usiku; mukafuna kufunsa, funsani, bwerani, idzani." Taurat Yesaya 21:11-12

Kodi **Duma** ndi ndani? Tiyeni tiwerengenso Taurat [Chipangano Chakale] kuti titsimikize kuti **Duma** yemwe watchulidwa ndi Yesaya mneneri'yu, anali m'modzi wa ana a **Ismayeli** kuchokera kumaiko akum'mawa. Pamene Yesaya ankatchula dzina la **Duma'li** nkuti patapita zaka 800 chimwalirire **Duma** mwini dzinali. Choncho, kutchulidwa kwa dzina la **Duma** m'nthawi ya Yesaya kunalibe chiri chonse chokhuzana ndi mwini dzinayu; ichi chikutitsimikizira kuti uwu unali ulosi wonena za mtsogolo; wa nthawi ya mapeto a dziko ino.

"Koma izi zinachitika kwa iwowa monga zotichenjeza, ndipo zinalembedwa kutichenjeza ife, amene matsirizidwe a nthawi ya pansi pano adafika pa ife." 1 Akorinto 10:11

Kawiri konse Duma akufunsa **mlonda, "Nthawi yanji ya usiku?"** Ngati njira yodzitchinjirizira kwa adani, kale alonda amaikidwa m'malo ofunikira a Yerusalemu . Anali ochenjeza anthu ngati kumabwera adani. Iwo samaodzera kapena kugona…

Lero alonda okhala pa malinga ndi anthu omwe apatsidwa Uthenga Wabwino aulalikire kwa amitundu onse mosabisa, kuchotsa kapena kuonjezera chiri chonse. Alonda okhulupirika ayenera kulichenjeza dziko lapansi, kuphatikiza Asilamu za chinyengo chachikuru chomwe chikusokeretsa anthu a mitundu yonse. A Seventh-day Adventist okhulupirika akhala akulalikira ku mapfuko onse a dziko lapansi za m'chitidwe wa bodza wa gulu lalikuru lomwe likunka likulimbikitsa ziphunzitso za chipembedzo chonama, pochita zozizwa zomwe zikunka zikufalikira ponseponse mofulumira kuti zisokeretse dziko lonse kulitengera kuchionongeko ngati silingachenjezedwe mokwanira. Tsono poyankha funso la Duma: 'Nthawi yanji ya usiku?' Alonda olungama a chi-Seventh-day Adventist akudziwa bwino kuti, "Kuli kucha." Iwo atangwanika kulalikira za m'mawa wamyaya wa tsiku lalikuru lomwe Isa al-Masih adzaturukira m'mitambo ya kumwamba pomwe diso liri lonse lidzamuona.

"Taonani, adza ndi mitambo; ndipo diso liri lonse lidzampenya Iye, iwonso amene anampyoza; ndipo mafuko onse a pa dziko adzamlira Iye. Terotu, Amen." Injeel Chibvumbulutso 1:7

Alonda akudziwa kuti tsiku

la kumapeto a nthawi, limene Isa adzaturukira, manda adzatseguka. Padzakhala kuukitsidwa kwa makamumakamu a anthu aturuke m'manda m'mene anagonamo, monga ananenera Isa al-Masih:

"Musazizwe ndi ichi, kuti ikudza nthawi, imene onse ali m'manda adzamva mau ake, nadzaturukira, amene adachita zabwino, kukuuka kwa moyo; koma amene adachita zoipa kukuuka kwa kuweruza." Injeel Yohane 5:28-29

Alonda okhulupirika a chi-Seventh-day Adventist akhala akulalikira uthenga wakubwera kwa tsiku lalikuru la myaya wosatha ndi momwe likonzekedwere. Kenaka iwo akhala akuyerekeza usana wa tsiku lalikurulo ndi mdima wa myaya wosatha ukudza pa osalungama. Usiku wa mdima wosungidwira onse akutsutsana ndi malamulo a Mulungu ndi umboni wa Yesu.

Alonda akufotokoza momveka kuti onse amene akufuna kuchoka m'misampha ya Satana, akhale ndi chikhulupiriro cha Yesu, chomwe ndi chilungamo cha khalidwe lake komanso cha moyo wake wangwiro. Tikadali m'nthawi ya mtendereyi, tiyeni tiyesetse kupanga ubale ndi Khristu. Uwu ungatheke pakupemphera moona mtima tsiku ndi tsiku ndi kuwerenga Mabuku a Mau Oyera, tikatero tidzachirimika m'ora la kuyesedwa ndi chizunzo ziri nkudza, ndi kukonzekera mokwanira kudzakomana naye Isa al-Masih m'mtendere, titabvekedwa mkanjo wa chilungamo chake.

"Ndipo kudzakhala kwa ife chilungamo, ngati tisamalira kuchita malamulo awa onse pamaso pa Yehova Mulungu wathu, monga anatilamulira ife." Taurat Deuteronomo 6:25

Ochita ichi adzakhala iwo amene "adalandira chikhulupiriro cha mtengo wake womwewo ndi ife, m'chilungamo cha Mulungu wathu ndi Mpulumutsi Yesu Khristu." Injeel 2 Petro 1:1

Nkhawa yathu ya tsiku ndi tsiku idzikhala: Kodi mtima wanga wakonzedwa mwatsopano? Moyo wanga wasinthika? Machimo anga akhululukidwa mwa chikhulupiriro mwa Khristu? Ndabadwanso mwatsopano mwa Mzimu wa Allah? Ndikugwirizana ndi maitanidwe ake akuti: "Idzani kuno kwa Ine nonsenu akulema ndi kuthodwa, ndipo Ine ndidzakupumulitsani inu."? Injeel Mateyu 11:28. Ndaziyesa zosayenera zonse kukhala zopanda pake chifukwa chokhala ndi chidziwitso cha Khristu Yesu? Ndikukhulupirira mau onse oturuka mkamwa mwa Mulungu?

"….dziwani kuti Yehova Mulungu wanu ndiye Mulungu; ndiye Mulungu wokhulupirika wakusunga chipangano ndi chifundo ndi iwo akumkonda ndi kusunga malamulo ake kufikira mibadwo zikwi." Taurat Deuteronomo 7:6-9.

Alonda alimbikitse kuti, "Munthu sadzakhala ndi moyo ndi mkate wokha, koma ndi mau onse akuturuka m'kamwa mwa Mulungu." Injeel Mateyu 4:4.

## ANENERA ZA ARABIA

"Ulosi wokhuza Arabia: M'nkhalango ya m'Arabia mudzagona, inu makamu oyendayenda a Dedani. Muchingamire akumva ludzu ndi njara; okhala m'dziko la Tema ananka kukomana ndi othawa ndi chakudya chao. Pakuti iwo anathawa malupanga, malupanga osololedwa, ndi mauta olifuka ndi nkhondo yobvuta." Yesaya 21:13-15 TNIV

Kodi kuitana kumeneku kukuimira nthawi imene Mulungu adzaitana mwana woyamba kubadwa wa Abrahamu, Ismayeli, yemwe adzauzidwa kubweretsa chakudya ndi madzi kwa iwo othawa nkhondo ya uzimu ya m'masiku otsiriza? Inde. Komanso



kukuimira anthu a maiko akumadzulo amene adzapeza chitchinjirizo mwa Asilamu mu nthawi yakukakamizidwa kwa "chilembo cha chirombo." Okana ichi adzaumirizika kuthawa, chifukwa ulosi ukuti iwo sadzaloredwa kugula kapena kugulitsa. Adzathawira kuti? Ena a anthu amaiko akum'mawa adzatsegula mitima ndi makomo ao kuwalandira anthu olungama omwe adzathawire m'maiko ao pofuna kupulumutsa miyoyo yao. Monga sipadzakhala kulumikizanika kuli konse pakati pa olungama ndi mphamvu ya Mulungu yakuwapulumutsa mu nthawi yakusowa thandizoyi? Padzakhala. Yense wofuna kumvetsetsa za chomwe chidzachitika awerenge bukhu la Greta Controversy [Mkangano Waukuru} lolembedwa ndi E. G. White. Bukhu'li ndi lofunikira kuti munthu aliyense kuphatikiza pokhala nalo aliwerenge m'nthawi yakumapeto ino.

## YESU M'KORANI

Anthu ambiri akufunitsitsa kudziwa kuti kodi Yesu Mwana wa Mariya ndi ndani? Nanga Koran Lolemekezeka ndi Bukhu Lopatulika amati chiyani za Iye?

Yesu/Isa ndiye "njira" (*al sirat mustaqueem*); Sura 43:61.

Yesu/Isa ndiye "choonadi" (al haq); Sura 19:34.

Yesu/Isa ndiye "moyo" (*Min Rouhina*); Sura 21:91, 66:12.

"Yesu ananena naye, Ine ndine njira, ndi choonadi ndi moyo. Palibe munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine." Injeel Yohane 13:6.

Ulosi uwu wonena za Isa unalaulidwa ndi Yesaya mneneri zaka 700 Isa al-Masih asanabadwe:

"Chifukwa chake Ambuye mwini yekha adzakupatsani inu chizindikilo; taonani namwali adzaima, nadzabala mwana wamwamuna, nadzamutcha dzina lake Imanueli." Taurat Yesaya 7:14

Panali amuna a ku m'mawa kwa Yerusalemu omwe anawerenga Malembo Oyera akale a chi-Hebri. Poona "nyenyezi" kum'mawa anakumbukira mau anawerenga m'Malembawo: "…Idzaturuka nyenyezi m'Yakobo…" Taurat Numeri 24:17. Amunawo analimbikitsidwa kuti nyenyezi anaionayo inali chizindikilo cha Mulungu kuti anatumiza Wina Woposa ku dziko lapansi. Pamene anawerenga maulosi onena za Isa al-Masih ibn Maryam, mobwerezabwereza, anatsimikizika mtima kuti Mulungu anawaonetsera iwo kuti Iye anatumiza ku dziko lapansi munthu woposa onse. Anzeru amenewa anamva chikakamizo chakuti anyamuke kutsatira kuli konse kumene nyenyeziyo inawatsogolera.

Iyo inawatsogolera ku Yerusalemu. Pamene anafika, anawafunsa Ayuda, "Ali kuti amene anabadwa Mfumu ya Ayuda? Chifukwa tinaona nyenyezi yake kum'mawa, ndipo tinadzera kudzamlambira Iye." Injeel Mateyu 2:2.

"Ndipo anauza iwo, 'M'Betelehemu wa Yudeya; chifukwa kunalembedwa kotere ndi mneneri….," Mateyu 2:5. "Ndipo iwe Betelehemu Efrata, ndiwe wamng'ono kuti ukhale mwa zikwi za Yuda, mwa iwe mudzandituturukira wina wakudzakhala woweruza m'Israyeli; maturukiro ake ndiwo a kale lomwe, kuyambira nthawi yosayamba. Mika 5:2 LITV

Anzeruwo ananyamuka kunka ku Betelehemu, ndipo m'mene anali kuyenda, nyenyezi inaonekaranso niwatsogolera iwo ku malo kumene Isa anabadwira. "Ndipo pofika ku nyumba anaona kamwanako ndi Mariya amake, ndipo anagwa pansi namgwadira Iye. Namasula chuma chao, nampatsa Iye mitulo, ndiyo golide, libano ndi mure." Injeel Mateyu 2:11 NLT

Koran Lolemekezeka limafotokoza kuti Yesu Mwana wa Mariya anali munthu woposa onse ndipo modabwitsa anabadwa mwa namwali wotchedwa Maryam, nakhala munthu. (fayakum).

" Iye [Mariya] anati, 'Inu Ambuye wanga! Ndidzakhala bwanji ndi mwana wamwamuna ine popeza sindidziwa mwamuna?' Iye anayankha: Ngakhale kuli tero: Mulungu amachita chiri chonse chimene wafuna: Iye akakhazikitsa chinthu, Amati kwa icho, "Uchitike," ndipo chimachitika." Sura 3.47 Aal-E-Imran.

"Iye [Mariya] anati, 'Ndikhala bwanji ndi mwana wamwamuna pokhala ine wosadziwa mwamuna, popeza ndine namwali?'"

"Ndipo (kumbukirani) iye (Mariya) anali woyera unamwali wake wonse: Tinapumira (m'mimba mwake) **Mzimu Wathu**; natsimikizira za choonadi cha mau a Ambuye analankhulidwa kwa iye….." Sura 66.12 At-Tahrim

"Ndipo kubadwa kwake kwa Yesu Khristu kunali kotere: Amai wake Mariya anapalidwa ubwenzi ndi Yosefe, koma **asanakomane iwowo, anapezedwa iye ali ndi pakati mwa Mzimu Woyera.**" Injeel Mateyu 1:18

Chipangano Chatsopano [Injeel] chikutsimikizira ulosi wa Yesaya kuti Yesu anabadwa mwa namwali.

"Ndipo mwezi wachisanu ndi chimodzi mngelo Gabrieli anatumidwa ndi Mulungu kunka ku mudzi wa ku Galileya dzina lake Nazarete, kwa namwali wopalidwa ubwenzi ndi mwamuna, dzina lake Yosefe, wa pfuko la Davide ndipo dzina la namwaliyo ndi Mariya. Ndipo pakulowa mngelo anati kwa iye, Tikuoneni wachitidwa chisomo, Ambuye ali ndi iwe. Koma iye ananthunthumira ndi mau awa, nasinkhasinkha kulankhula uku nkutani. Ndipo mngelo anati kwa iye, 'Usaope, Mariya; pakuti wapeza chisomo ndi Mulungu. Ndipo taona, udzakhala ndi pakati, nudzabala mwana wamwamuna, nudzamutcha dzina lake Yesu. Iye adzakhala wamkuru, nadzatchedwa Mwana wa Wamkurukuru.'

" Koma Mariya anati kwa mngelo, 'Ichi chidzachitika bwanji, popeza ine sindidziwa mwamuna? Ndipo mngelo anayankha, nati kwa iye, 'Mzimu Woyera udzafika pa iwe, ndi mphamvu ya Wamkurukuru idzakuphimba iwe: chifukwa chakenso Choyeracho chidzabalidwa, chidzatchedwa Mwana wa Mulungu.'" Injeel Luka 1:26-35 TNIV

## ISA, MPHATSO YA MWANA WAMWAMUNA WOYERA

"Ndipo iye [mngelo wa Mulungu] anati, "Usatero, ine ndine wotumidwa kuchokera kwa Ambuye wako, ( kudzafotokoza) **kwa iwe za mphatso ya mwana wa mwamuna woyera.**" Sura 19:19.

Mariya, Iye ali wochokera mwa Mzimu wa Mulungu (*Rouhana Allah*): Sura 19:17; 21:91: 66:12.

Mzimu wa/wochokera kwa Mulungu (*Rouh minhu Allah*): Sura 4:171.

Iye anapatsidwa mphamvu/ kutsogozedwa (*ayyadhu*) ndi Mzimu Woyera (*Rouh Qudus*): Sura 2:87; 2:253; 5:110.

"…Tinampatsa Yesu mwana wa Mariya Machitidwe (Zizindikilo) ndi kumtsogolera iye ndi mzimu woyera…" Sura 2:87 Al-Baqara

."Pomwepo Mulungu adzati, 'Ha! Yesu mwana wa Maryamu! Werenga madalitso anga kwa iwe ndi kwa mai wako. Taona! Ndinakutsogolera iwe ndi mzimu woyera... Taona! Ndinakuphunzitsa iwe Bukhu (Lopatulika) ndi luntha ndi Uthenga Wabwino…ndipo ukutha kuchiritsa ngakhale iwo obadwa osapenya, ndi akhate mwa mphamvu yangayo. Ndipo taona! ukuthanso ngakhale kuukitsa akufa mu mphamvu yanga yomweyo…" Sura 5:110 Al-Maeda.

Yesu Mpulumutsi ali uthenga wabwino ndi mau opatsa moyo ochokera kwa Mulungu."Taona! Anapfuula angelo, 'Ha! Mariya! Mulungu **wakutumizira iwe uthenga wokondweretsa wa Mau yemwe wachokera kwa Iye: dzina lake adzatchedwa Yesu Mpulumutsi, Mwana wa Mariya,** wolemekezedwa m'dziko lino ndi m'ilo lirinkudza komanso ndi onse (khamu la iwo) akukhala **chifupi ndi Mulungu**. Sura 3:45 Aal-E-Imran.

"Ndipo mngelo anati kwa iwo [abusa], Musaope; pakuti onani, ndikuuzani inu uthenga wabwino wa **chikondwerero chachikuru,** chimene chidzakhala kwa anthu onse." Injel Luka 2:10 MKJV.

Yesu/Isa ali Mau a Allah (*Kalimatu Allah*): **Mau Ake**: Sura 3:39; 3:45; 4:171.

"Yesu Mpulumutsi mwana wa Mariya anali…mtumiki wa Mulungu ndiponso **Mau Ake…**" Sura 4:171 An-Nisa.

"Pachiyambi panali **Mau**, ndipo **Mau** anali kwa Mulungu, ndipo **Mau ndiye Mulungu**." Injeel Yohane 1:1 TNIV.

"**Ndipo Mau anasandulika thupi**, nakhazikika pakati pa ife, ndipo tinaona ulemelero wake, ulemelero wonga wa wobadwa yekha wa Atate, wodzala ndi chisomo ndi choonadi." Injeel Yohane 1:14 TNIV.

Isa anali mwana woyera, wopanda uchimo (*zakiyyah*), wolungama. Sura 3:46; 19:19.

Analibe chinyengo kapena chidetso chiri chonse. Sura 19:23.

Ali wolungama (*saliheen*): Sura 3:46; 6:85.

Moyandikitsitsa ndi Mulungu (*muqarrabeen*, kumalo a ulemu wapadera); ndi yekhayo akufotokozedwa kuti anapatsidwa ulemu wakutero m'Koran: Sura 3:45 Aal-E-Imram.

"Kale **Mulungu** analankhula ndi makolo athu mwa aneneri m'manenedwe ambiri ndi mosiyanasiyana, koma pakutha pake pa masiku ano analankhula ndi ife ndi Mwana amene anamuika wolowa nyumba wa zonse, mwa Iyenso analenga maiko ndi am'mwamba omwe; ameneyo, pokhala ndi chinyezimiro cha ulemelero wake, ndi chizindikilo chenicheni cha chikhalidwe chake, nanyamula zonse ndi mau a mphamvu yake, m'mene adachita chiyeretso cha zoipa, anakhala pa dzanja lamanja la Ukulu m'Mwamba." Injeel Ahebri 1:1-3.

Yesu ali chifanizo ndi chenicheni cha Mulungu, chotsimikizira amitundu za khalidwe langwiro la Mulungu, ndi chotionetsera momwe tiyenera kukhalira kuti tifanane ndi Mulunguyo. Mwa Yesu tikumuona Mulungu monga ali.

Yesu ali nkhoswe/yolemekezeka/ yokwezeka (*wajiham* kapena *wajih*) ya moyo uno ndi ulinkudza. (Uwutu ndi ulemu womwe wapatsidwa kwa Yesu ndi Mose omwe akuimira atumiki a mapangano awiri). Sura 3:45.

Ndi yekhayo mtetezi (*shalafa'a*). Sura 2:255; 21:28.

"**Pakuti pali Mulungu mmodzi, ndi Mtetezi mmodzi pakati pa Mulungu ndi anthu,** ndiye munthu **Yesu Khristu.** Injeel 1 Timoteo 2:5.

Iye ali njira ya chilungamo (*siratun mistaqueem*): Sura 3:51; 4:61.

Ali chinsinsi cha wosaonekayo (*ghyab*) (wosalengedwa): Sura 3:44.

Chikondi cha Mulungu chinaotsedwa mwa iye: Sura 5:110; 43:59.

Mulungu anamdalitsa (*mubarak*) iye pali ponse pomwe anakhala; Sura 19:31.

Napatsidwa iye nzeru ndi mabvumbulutso a Chipangano Chakale ndi Uthenga wabwino: Sura 3:48; 2:136; 19:30; 43:63; 57:27.

Mulungu anabvumbulutsa chifuniro chake kwa Yesu/Isa: Sura 4:163.

Natchedwa Khristu: Sura 3:45; 4:157; 4:171; 4:172; 5:17 (kawiri), 5:72 (kawiri), 5:75; 9:30; 9:31.

Nakhala "chifundo chochokera kwa Mulungu" (*rahmatun*): Sura 19:21.

Anali chitsimikizo chenicheni (*be-yinat*, kutanthauza "woona ndi wopanda chokhumudwitsa") kwa anthu (mtundu wonse wa anthu): Sura 2:87; 19:21; 21:91; 43:61.

Anachiritsa akhungu ndi akhate: Sura 3:49; 5:110.

Anali ndi mphamvu youkitsa akufa: Sura 3:49; 5:110.

Mozizwitsa amapatsa dziko lapansi chakudya chochokera kumwamba: Sura 5:112-115.

Anthu anapangana (kutsutsana naye): Sura 3:54.

Iye anachitiridwa umboni wonama: Sura 3:55.

Anafa (*mutawafeka* liu lochokera ku verebu la chi-Arabu *tawwafa* [anaphedwa] pamene *amutu* likuchokera ku *mata* (anafa): Sura 3:55; 4:159; 5:117; 19:33.

"Anawafera osapembedza." Injeel Aroma 5:6.

"Khristu anatifera ife." Injeel Aroma 5:8.

"Adafera, nakhalanso ndi moyo…" Injeel Aroma 14:9.

"Khristu anafera zochimwa zathu." Injeel 1 Akorinto 15:3.

Anauka kwa akufa (*yum uba'athu*): Sura 19:33.

Anakwera kumwamba kwa Mulungu; Sura 3:55; 4:61.

Adzabweranso pa tsiku lachiweruzo (*yum al-qiyama*): Sura 3:55; 4:159; 43:61.

Chizindikilo cha, ndi Wodziwa za ora la chiweruzo: Sura 43:61.

Wamithenga/mtumwi (*rasul*); Sura 4:157; 5:75.

Mneneri (*nabbyun*) wa Mulungu: Sura 19:30.

Mtumiki (*abd Allah*) wa Mulungu: Sura 4:172; 19:30; 43:59.

Mboni (*shahid*) yokhulupirika ya Mulungu: Sura 4:159; 5:117.

Mtendere (*salaam*) ukhala pa iye: Sura 19:33.

Atumwi ndi antchito anzake a Mulungu (*ansar Allah*) anafalitsa chibvumbulutso cha Yesu/Isa: Sura 3:52; 61:14.

Atumwi ali mboni za choonadi cha Yesu/Isa: Sura 5:113.

Tikulamulidwa ife kumvera (*alee'uon*) iye; Sura 3:50; 43:63.

## KODI ISA AL-MASIH IBN MARYAMU NDI NDANI?

Isa al-Masih Ibn Maryamu ali chifanizo changwiro cha Mulungu, Mulungu wokhala m'thupi la umunthu. Kudzera mwa iye ife timamvetsetsa chenicheni chomwe Mulungu ali.

"Khristu Yesu ali…wofanana m'zonse ndi Mulungu": Sura 3:45 Aal-E-Imram.

"Mwana ali chinyezimiro cha ulemelero wa Mulungu, ndi chizindikilo chenicheni cha chikhalidwe chake, nanyamula zonse ndi mau a mphamvu yake m'mene adachita chiyeretso cha zoipa, anakhala pa dzanja lamanja la Ukulu m'Mwamba." Injeel Ahebri 1:3 TNIV.

"Kulibe munthu anaona Mulungu nthawi zonse; Mwana wobadwa yekha wakukhala pa chifuwa cha Atate, Iyeyu anafotokozera." Injeel Yohane 1:18 NLT.

Yesu Mpulumutsi ndi yekhayo amene ali mmodzi, wosati nkulekanitsika, ndipo akhala, nthawi zonse pamaso pa Mulungu.

"Palibe munthu waona Atate, koma Iye amene ali wochokera kwa Mulungu, ameneyo waona Atate." Yoh. 6:46. TNIV.

Yesu amamuonetsera Atate wake kudzera m'khalidwe la moyo wake.

Yesu ananena naye, Kodi ndiri ndi inu nthawi yaikuru yotere, ndipo sunandizindikira, Filipo? Iye amene wandiona Ine waona Atate; unena bwanji, Mutionetsere Atate?" Injeel Yohane 14:9 MKJV.

"Pakuti mwa Iye [Yesu] chikhalira chidzalo cha Umulungu m'thupi." Injeel Akolose 2:9.

Yesu ali "Mau a Mulungu," Sikofunika kudziwa chomwe Yes ali kokha, komanso kumvetsetsa chomwe iye anaphunzitsa. Koran ndi Bukhu Lopatulika zimati Yesu Mpulumutsi ali Mau a Mulungu! Pouchitira chifundo mtundu wa anthu, Yesu anatumizidwa kudzakhala chitsanzo chathu m'makhalidwe ndi chiphunzitso za chenicheni chimene Mulungu ali. Anabwera kutithandiza kuimvetsetsa njira ya kumwamba. Inde, powachitira chisoni anthu Yesu anatumidwa pansi pano! Tikafuna kumvetsetsa za Mulungu, tiwerenge zomwe Isa anaphunzitsa ndi momwe anakhalira moyo wake.

## KODI ISA ANAPHUNZITSA CHIYANI?

Kufotokza mwachidule zomwe Isa anaphunzitsa. Aliyense akhale ndi Chipangano Chatsopano, maka cholembedwa m'chilankhulo chake, kuti athe kudziwerengera yekha. Yesu kunapatsidwa Uthenga Wabwino kapena "Mau abwino, osangalatsa a chipulumutso kuchokera kwa Mulungu." Dzipezereni Chipangano Chatsopano cha ulere kuchokera pa **www.e-sword.org**

"…Pambuyo pao tinatumiza Yesu, yemwe tinampatsanso Uthenga Wabwino: Tinalonga m'mitima mwa omtsatira Chifundo ndi Chisoni… koma ambiri [a omtsatirawo] anaukira nachimwabe." Sura 57:27 Al-Hadid.

" Ndi Iye amene anatumiza kwa inu Bukhu Lopatulika m'choonadi, (pang'onopang'ono), anaphunzitsa zomwe zinachitika pachiyambi lisanalembedwe ili; ndipo anatumiza chilamulo (cha Mose) ndi Uthenga Wabwino (wa Yesu) Bukhu lisanakhale, kukhala zotsogolera anthu, natumizanso machitidwe otha kulekanitsa (chabwino ndi choipa).

Sura 3:3 Aa-E-Imram.

"Ndipo monga mwa mayendedwe ndi machitidwe a [aneneri akale], Tinatumiza Isa mwana wa Maryamu, kudzakwaniritsa chilamulo chomwe chinaperekedwa Iye asanabadwe: Tinampatsa Iye Uthenga Wabwino; momwe muli malangizo ndi kuunika, ndiponso chikhaszikitso cha Malamulo omwe anaperekedwa Iye asanadze, kukhala chotsogolera ndi chenjezo kwa iwo oopa Allah." Sura 5:46 Al-Maeda.

"Akadakhala kuti iwo [Anthu a Bukhu] anasunga chisungire Malamulo, namvera Uthenga Wabwino ndi mabvumbulutso omwe anaperekedwa kwa iwo kuchokera kwa Mulungu, akanadzala ndi kusekera m'moyo wao wonse. Koma ndi kagulu kakang'ono komwe kakuchita bwino pakati pao; ochuruka a iwo akuyenda m'njira za uchimo." Sura 5:66 Al-Maeda.

"Pfuula ndi kunena, 'Ha, inu anthu a Bukhu [Akhristu]! Mulibe maziko oimapo pokhapokhapo mukadaima osagwedezeka pa Malamulo, Uthenga Wabwino, ndi mabvumbulutso onse omwe anadza kwa inu kuchokera kwa Mulungu wanu.' Ndi mabvumbulutso omwe anapatsidwa kwa inu kuchokera kwa Ambuye, omwe amathandiza onse oopa Mulungu kuti asampandukire ndi kumchitira mwano." Sura 5:68 Al-Maeda.

Mu Uthenga Wabwino timaphunziramo chifuniro cha Mulungu pa anthu onse. Tawerengani mitu ya Mateyu 5 ndi 6:

"Ndipo m'mene Iye anaona makamu, anakwera m'phiri; ndipo m'mene Iye anakhala pansi, anadza kwa Iye ophunzira ake; ndipo anatsegula pakamwa, nawaphunzitsa iwo nati, Odala ali osauka mumzimu; chifukwa uli wao Ufumu wa Kumwamba. Odala ali akufatsa; chifukwa adzalandira dziko lapansi. Odala ali akumva njala ndi ludzu la chilungamo; chifukwa adzakhuta. Odala ali akuchita chifundo; chifukwa adzalandira chifundo. Odala ali oyera mtima; chifukwa adzaona Mulungu. Odala ali akuchita mtendere; chifukwa adzatchedwa ana a Mulungu. Odala ali akuzunzidwa chifukwa cha chilungamo; chifukwa uli wao Ufumu wa Kumwamba. Odala muli inu m'mene adzanyazitsa inu, nadzazunza inu, nadzakunenerani monama zoipa ziri zonse chifukwa cha Ine. Sekerani, sangalalani: chifukwa mphotho yanu ndi yaikuru m'Mwamba: pakuti potero anazunza aneneri anakhalawo musanabadwe inul

" Inu ndinu mchere wa dziko lapansi; koma mcherewo ngati ukasukuluka, adzaukoleretsa ndi chiyani? Pamenepo sungakwanirenso kanthu konse, koma kuti ukaponyedwe kunja, nupondedwe ndi anthu. Inu ndinu kuunika kwa dziko lapansi. Mudzi wokhazikika pamwamba pa phiri sungathe kubisika. Kapena sayatsa nyali, ndi kuibvundikira m'mbiya, koma aiika iyo pa choikapo chake; ndipo iunikira onse ali m'nyumbamo. Chomwecho muwalitse inu kuunika kwanu pamaso pa anthu, kuti pakuona ntchito zanu zabwino, alemekeze Atate wanu wa Kumwamba. **Musaganize kuti ndinadza Ine kudzapasula chilamulo kapena aneneri: sindinadza kupasula, koma kukwaniritsa.** Pakuti indetu ndinena kwa inu**, Kufikira litapirira thambo ndi dziko, kalemba kakang'ono kamodzi kapena kansonga kake kamodzi sikadzachokera kuchilamulo, kufikira zitachitidwa zonse."**

## MINDA YA MYAYA

Tidzikumbukira nthawi zonse kuti dziko lapansi'li sikwathu. Mulungu watikonzera ife malo abwino, kumwamba, komwe Iye akufuna tonse okhala pa dziko tikakhaleko. Zachisoni, anthu ochuruka akukana kukhala pansi pa ulamuliro wa Mulungu ndi Malamulo ake a chilungamo; Malamulo Khumi, kapena kumlandira Yesu monga Mpulumutsi ku machimo ao. Koma kwa olungama omwe abvomera kumvera malamulo a Mulungu, kudzapatsidwa mphotho: "**Minda ya Myaya** yomwe adzayendamo: kunsi kwa mindayo kudzayenda mitsinje (yosefukira ndi chimwemwe): iwo adzalandira momwemo chiri chonse moyo wao udzachifuna: umu ndimo Allah adzapatsire mphotho kwa olungama." Sura 16:31 An-Nahl.

Mulungu akufunitsitsa kuti inu ndi ine tidzapezeke kumwamba. Iye watipatsa ife malonjezano oposa m'Mabuku Ake Oyera kuti tisalephere kudzapezeka kumeneko. Kodi ndife okonzeka kumlora Mulungu kuchita chifuniro chake m'moyo wathu? Malonjezano a m'Mabuku Oyera ake ndi okhulupirika ndithu.

"Ndipo ndinamva mau akuru ochokera ku mpando wachifumu, ndi kunena Taonani, chihema cha Mulungu chiri mwa anthu; ndipo adzakhalitsa nao, ndi iwo adzakhala anthu ake, ndi Mulungu yekha adzakhala nao, Mulungu wao; ndipo adzawapukutira misozi yonse kuichotsa pamaso pao; ndipo sipadzakhalanso imfa; ndipo sipadzakhalanso maliro, kapena kulira, kapena chowawitsa; zoyambazo zapita." Injeel Chibvumbulutso 21:3-4.

Okondedwa awerengi, kuli konse komwe muli, Mulungu ali ndi chidwi chachikuru za chipulumutso chathu. Kodi sitingathe ife kudalira pa Iye kotheratu, amene anatumiza Isa al-Masih mwana wa Maryamu kuchokera kumwamba kubwera pa dziko lapansi lodzala ndi uchimo'li kuti adzatipatse chiyembekezo cha moyo wosatha?

Ndi pemphero ndi cholakalaka cha mtima wanga kuti inu ndi ine tidzapezeke pakati iwo amene adzakhale m'minda yamyaya yomwe watikonzera Mulungu.

## NJIRA YOPAPATIZA

Tidzipemphera moona kuchokera pansi pa mtima kuti Mulungu mwa chisomo chake atipatse chidziwitso chokwanira cha "njira ya chilungamo." Njira zambiri za moyo uno ndi zotsogolera kuchitayiko. Tipemphere kosalekeza kwa Mulungu pemphero (*dua*) lakuti adzititsogolera "m'njira ya chiyero" yomwe Yesu Mpulumutsi mwana wa Mariya, anaitcha, "**njira yopapatiza,**" "**chipata chopapatiza**" chotsogolera ku moyo wosatha." Injeel Mateyu 7:13-14.

Tisadzinyenge pokhala ntambasale ndikudzinamiza kuti tapulumuka kale ku machenjerero a mdyerekezi. Koma tifunitsitse kuyenda modzichepetsa pamaso pa Mulungu, ndi kulingirira zakufunitsitsa kwathu nzeru ndi mphamvu zake. Tisaiwale kuti Satana anayambira kumwamba komweko, kusokeretsa angelo ochuruka amene kale lonse anamvera Mulungu, m'kuukira kwakukuru komwe kunali kusanachitikepo chilengedwere miyamba, iye anawapandutsa iwo kukhala kumbali yake.

"Ndipo chinaoneka chizindikilo china m'mwamba, taonani, chinjoka chofiira, chachikuru, chakukhala nayo mitu isanu ndi iwiri, ndi nyanga khumi, ndi pamutu pake nduwira za chifumu zisanu ndi ziwiri. Ndipo mchira wake uguza limodzi la mgawo atatu a nyenyezi zam'mwamba nuziponya padziko…" Chibv. 12:3-4.

Tsono popeza Satana anaponyedwa kunja kuchokera Kumwamba, iye analitenga dziko lapansi kukhala likuru lake.

"Ndipo munali nkhondo m'mwamba. Mikayeli ndi angelo ake akuchita nkhondo ndi chinjoka; chinjokanso ndi angelo ake chinachita nkhondo; ndipo sichinalakika, ndipo sanapezekanso malo ao m'mwamba. Ndipo chinaponyedwa pansi chinjoka chachikuru, njoka yokalambayo, iye wotchedwa mdierekezi ndi Satana, wonyenga wa dziko lonse; chinaponyedwa pansi kudziko, ndi angelo ake anaponyedwa naye pamodzi." Injeel Chibvumbulutso 12:7-9.

Satana anachita chipambano posokeretsa makolo oyambawo chifukwa iwo anamvetsera ku machenjerero ake:

"…Onse awiri anadya chipatso cha mtengo, pomwepo umariseche wao unaonekera kwa iwo: nasoka pamodzi iwo, kuyesa chobvala chao, masamba a m'Munda: umu ndimo anachimwira Adamu posamvera Mulungu wake, ndikulora kusokeretsedwa mmwini yekha." Sura 20:121 Ta-Ha

Satana akugwiritsabe ntchito machenjerero omwewo kusokeretsa anthu omwe lero alibe chitchinjirizo cha Mulungu.

"Ndipo ndinaona moturuka m'kamwa mwa chinjoka, ndi m'kamwa mwa chirombo, ndi m'kamwa mwa mneneri wonyenga mizimu itatu yonyansa ngati achule; pakuti ali mizimu ya ziwanda zakuchita zizindikilo; zimene zituruka kumka kwa mafumu a dziko lonse, kuwasonkhanitsira ku nkhondo ya tsiku lalikuru la Mulungu, Wamphamvuyonse." Injeel Chibv. 16:13-14.

Tizindikire ife kuti pa ntchito yake yosokeretsa anthu, Satana ndi atumiki ake akugwiritsa ntchito magulu atatu: chinjoka (atsogoleri a za chuma ndi a ndale omwe samaopa Mulungu koma ndi a chipembedzo cha Satanayo), chirombo (Upapa wa Aroma), ndi mneneri wonyenga (mipingo ya Mpanduko youkira Mulungu ya m'USA).

### UTHENGA WA ANGELO ATATU: CHENJEZO LOTSIRIZA

Pofuna kuitsiriza ntchito yake, Mulungu mwa chifundo chake chochuruka watipatsa mauthenga atatu "otchedwa Uthenga wa Angelo Atatu," alalikidwe kwa anthu onse m'nthawi yakumapeto ino, ndi cholinga chotipulumutsa kumachenjerero a Satana. Okondedwa, mauthengawa ndi otsiriza palibenso ena. Isa analandira mauthengawa, nawabvumbulutsira kwa Yahaya (Yohane), mtumiki wa Mulungu mwa mngelo Wake. Yahaya anawalemba awa mu Injeel ya Chibvumbulutso cha Yesu (Chibvumbulutso 1:1). Mauthenga a ulosi'wa akufotokozanso za madalitso a Mulungu kwa anthu amene awalandire ndi kuchita zomwe aphunzitsidwa. Ali chenjezo lochokera kumwamba.

"Wodala iye amene awerenga, ndi iwo amene akumva mau achinenerocho, nasunga zolembedwa momwemo; pakuti nthawi yayandikira." Injeel Chibvumbulutso 1:3.

## UTHENGA WA MNGELO WOYAMBA

Mau a mngelo woyamba akuti tiope ndikumpatsa ulemu Allah. Chifukwa lafika ora la chiweruzo chake!

"Ndipo ndinaona mngelo wina alikuuluka pakati pa mlengalenga, wakukhala nao Uthenga Wabwino wosatha, aulalikire kwa iwo akukhala padziko, ndi kwa mtundu uli wonse ndi pfuko ndi manenedwe ndi anthu; ndikunena ndi mau akuru, Opani Mulungu, mpatseni ulemelero; pakuti **yafika nthawi ya chiweruziro chake**; ndipo mlambireni Iye amene analenga m'mwamba ndi mtunda ndi Nyanja ndi akasupe amadzi." Injeel Chibvumbulutso 14:6-7.

"Uthenga Wabwino wosathawu" unaperekedwa ulalikidwe pa dziko lonse: kwa "mtundu uli wonse, pfuko, manenedwe, ndi anthu. Palibe munthu adzaweruzidwa wosadziwa; tonse tidzadziwa chotsatira cha ntchito zathu. Mwa chifundo chake Allah watipatsa nthawi kuti tisamalire njira zathu kudzera mwa mauthenga'wa. Iye sadzaononga anthu osanawachenjeza. Chionongeko chidzachitika pa moyo uli wonse umene unakukana kuunika kwa choonadi ndikusankha mdima wa uchimo.



## ORA LA CHIWERUZIRO

Tikukhala m'ora la chiweruziro cha Mulungu lomwe silinakhalepo chilengedwere dziko lapansi. Tiri m'nthawi yomwe atumiki enieni a Mulungu, ndi a Yesu amene Mulungu'yo anamtuma, akutsimikizika za mbali yomwe ali.

M'Qur'an Wolemekezeka, mwafotokozedwamo kuti kale m'masiku a mneneri wa m'chipululu, ora la chiweruziro linanenedwapo kuti linayandikira, chikhalirecho linali patali.

"**Ora la chiweruziro liri pafupi**" Sura 51:01 Al-Qamar.

"Tsiku" kapena "**ora la chiweruziro**" latchulidwa koposa makumi asanu ndi atatu m'Koran Wolemekezeka, chitsimikizo kuti uthengawu siwamacheza.

Ulosi wa Yahaya wa ora lachiweruziro, woyembekezedwa kwa nthawi yaitali'wu, wakwanitsidwa ndipo ukuchititsa wachiweruziro womwe anauneneranso Danieli (Danieli 8:14) umveke bwino kwambiri.. Danieli ananenera za kuyeretsedwa kwa Kachisi kumwamba, komwe Isa akutumikira monga Mkuruwansembe. Danieli anafotokoza za ora la chiweruzo'li kuti linali kukhala pansi kwa bwalo lakumwamba ndi kufufuza m'mitima ya anthu. Khamu la okhala



kumwamba liri pa ntchito yosindikiza maina a atumiki enieni a Allah m'bukhu la moyo. Danieli anachitcha chiweruzirochi, "kulungamitsa" kwa malo opatulika.

"Mpaka masiku zikwi ziwiri mphambu mazana atatu usana ndi usiku; pamenepo malo opatulika adzayesedwa olungama." Danieli 8:14.

Ulosi wa ora la chiweruziwu unaperekedwa kwa Danieli m'Chipangano Chakale, kuti timvetsetse za nthawi yeniyeni linayambira. Bukhu Lopatulika likutitsimikizira kuti nthawi yakuyeretsedwa kwa Kachisi wakumwamba, inayamba pa October 22, 1884 A.D. Kuyambira apa chiweruziro cha nthawi-yachimaliziro anachinenera Danieli (Danieli 7:9-10) chikuchitika.

Okondedwa, izi zikutanthauza kuti zonse zomwe inu ndi ine tikuchita, kuganiza ndi kunena tsiku liri lonse zikuweruzidwa. Kodi timalingaliranji tikakhala? Nanga chikondi chathu chakhazikika pa chiyani? Monga takhazikika pa Mulungu? Kapena takhazikika kwambiri ku ntchito za malonda zodzikundikira chuma cha dziko lapansi?

"Maso a Yehova ali pa olungama mtima, ndipo makutu ake atchereza kulira kwao. Nkhope ya Yehova itsutsana nao akuchita zoipa, kudula chikumbukilo chao pa dziko lapansi." Masalmo 34:15-16.

Ulosi wa chenjezo la chiweruziro'wu, molumikizana ndi mauthenga a angelo ena, udzapherezera pa tsiku lakubwera kwa Isa al-Masih mwana wa Maryamu m'mitambo ya kumwamba. Choncho kulalikidwa kwa uthenga wa chiweruzirowu kulinso kulalikira kwa uthenga wakubwera kwachiwiri kwa Isa kuti kwayandikitsa. Uthenga umenewu ukutchedwa uthenga wabwino wosatha. Chikangotha chiweruziro chakufufuza a amoyo ndi akufa, Isa akubwera pa dziko lapansi kudzadzisonkhanitsira kwa Iye yekha onse amene anamlemekeza Iye pakuchita chifuniro chake. Adzatenga olungama onse kunka nao kumwamba.

Koran Wolemekezeka akufotokoza kuti Yesu ali "chizindikilo" chakukwanitsidwa kwa ora la chiweruziro.

"Ndipo (Yesu) adzakhala Chizindikilo (cha kukwanitsidwa kwa) Ora (la chiweruziro): choncho musakhalenso ndi chikaiko za (Ora'lo), koma inu munditsate Ine: komwe ndi Njira yokhayo yoongoka." Sura 43:61 Az-Zukhruf

## MLAMBIRENI MLENGI

Uthenga wa mngelo woyamba – momwenso muli za "kufika kwa ora la chiweruzo" – ukufotokozeranso anthu onse a pa dziko kuti "mlambireni Iye amene analenga m'mwamba ndi mtunda ndi nyanja ndi akasupe amadzi." Chibvumbulutso 14:7.

Mau awa akungotikumbutsa za Malamulo Khumi a m'Chipangano Chakale. Maka za lamulo la chinai lomwe limati Mulungu ndiye Mlengi wa "zakumwamba ndi zapansi, ndi nyanja, ndi zinthu zonse ziri m'menemo." Taurat Eksodo 20:11.

Ndi zochititsa chidwi kwambiri kuti lamulo limene linakhala likinyalanyazidwa ngati lopanada ntchito koma poperekedwa kwa Mose linayambidwa ndi liu "uzikumbukira." Mu uthenga wa mngelo woyamba wa Chibvumbulutso 14:7 ifenso tikulangizidwa "kumbukira" Sabata (As-Sabt), la tsiku lachisanu ndi chiwiri, kuti likhale lopatulikira Mulungu, komanso lakukumbukira ntchito yake ya kulenga. Choncho tizililemekeza ilo ndi "kumpembedza Iye" ndipo mosanyinyirika tisiye ntchito zathu ndi kupumula pa la Sabata liri lonse.

Lamuloli linalembedwa ndi chala cha Mulungu mochita kuzokota pamagome a miyala.

"Ndipo atatha Iye kulankhula ndi Mose, pa phiri la Sinai, anampatsa magome awiri a mboni, magome a miyala, olembedwa ndi chala cha Mulungu." Taurat Eksodo 31:18

Mau analembedwapo anali:

"**Uzikumbukila tsiku la Sabata, likhale lopatulika. Masiku asanu ndi limodzi uzigwira, ndi kumariza ntchito zako zonse; koma tsiku lachisanu ndi chiwiri ndilo Sabata la Yehova Mulungu wako; usagwire ntchito iri yonse**, kapena iwe wekha, kapena mwana wako wamwamuna, kapena mwana wako wamkazi, kapena wantchito wako wamwamuna, kapena wantchito wako wamkazi, kapena nyama zako, kapena mlendo amene ali m'mudzi mwako; chifukwa masiku asanu ndi limodzi Yehova adamariza zakumwamba ndi zapansi, ndi nyanja, ndi zinthu zonse ziri m'menemo, napumula tsiku lachisanu ndi chiwiri; chifukwa chake **Yehova anadalitsa tsiku la Sabata kuti likhale lopatulika**." Taurat Eksodo 20:8-11.

Lero unyinji wa anthu okhala pa dziko sakusamala konse za tsiku lakupumula la chisanu ndi chiwiri la pa mulungu – lomwe Mulungu pa Chilengdwe pomwe analipatura ndi kulipatsa ku mtundu wa anthu. Ichi nchifukwa chake chenjezo lomwe linaperekadwapo m'nthawi ya Nowa, likuperekedwanso kwa anthu tonse a dziko lapansi ndi maunso akuti "Mlambireni Iye...analenga m'mwamba ndi ntunda ndi nyanja ndi akasupe anadzi" kutanthauza chimodzimodzi, "Uzikumbukira Tsiku la Sabata." Kuchita chifuniro cha Mulungu ndiko kumpembedza Iye. Kukhala m'maonekedwe a mitundu mitundu a chipembedzo, sindiko kupembedza Mulungu koyenera koma kumvera ndi kuchita Mau ake nthawi zonse ndiko. Samueli akufotokoza kuti,

"...Kodi Yehova akondwera ndi nsembe zopsereza ndi nsembe zophera, monga ndi kumvera mau a Yehova? Taonani, kumvera ndiko kokoma koposa nsembe, kutchera khutu koposa mafuta a nkhosa zamphongo." 1 Samueli 15:22 NLT.

Kwa anthu ambiri, kumvera Mau a Mulungu kumangokhala pakulankhula kokha.

"Kumvera kwao kuli pa milomo yao..." Sura 4:81 An-Nisa

Koma zochita zao za usana ndi usiku ndi zolankhula zao ziwatsutsa kuti ndi osatsimikizika pa chikhulupiriro. M'nthawi ya mneneri Ezekieli Mulungu anadzudzulapo za maonekedwe achipembedzo abodzawa:

"Ndipo akudzera monga amadzera anthu, nakhala pansi pamaso pako ngati anthu anga, namva mau ako, koma osawachita; **pakuti pakamwa pao anena mwachikondi, koma mtima wao utsata phindu lao.**" Taurat Ezekieli 33:31

Pochita mantha kuti angachepetse phindu la m'ntchito zao za malonda, anthu ambiri lero amanyalanyaza lamulo la Mulungu lakupumula ku za dziko ndi kumtumikira Iye pa tsiku lachisanu ndi chiwiri. Tikadangomvera ndi kugonjera malamulo a Mulungu - Malamulo Khumi, ndi kumapumula molingana ndi lamulo lachinai, dziko lathu lapansi'li likadalitsidwa koposa.

"**Akanakhazikika iwo pa malamulo**, namvera Uthenga Wabwino ndi kutsatira bvumbulutso lomwe linapatsidwa kwa iwo ndi Mulungu, akadakhala anthu okondwa moyo wao wonse. Koma pali kagulu kochepetsetsa pakati pao kamene kakuyenda m'njira yolondora: ochuruka a iwo asankha njira yakuchionongeko." Sura 5:66

Al-Maeda.

Anthufe timatumikira Mulungu ndi milomo yathu yokha, pamene mitima yathu iri kutali ndi Iye. Yesu anadzudzulapo za machitidwewa:

"Anthu awa andilemekeza Ine ndi milomo yao; koma mtima wao uli kutari ndi Ine." Mateyu 15:8.

Kumvera ndi kuchita mau ndi malamulo a Mulungu, ndi kokhako komwe kumationetsera timamkonda. Koma machitidwe ali onse opembedza omwe mkati mwake mulibe kuchita Mau Ake ali chabe ndipo timangodzinyenga tokha.

## MNGELO WACHIWIRI: WAGWA, WAGWA, BABULO


Uthenga wachiwiri wa nthawi yachimariziro wa mngelo wachiwiri, ukulalikira za kugwa kwa mipingo yomwe poyamba inayenda m'choonadi koma tsopano yachitaya. Pakutaya choonadicho yapangitsa kuti, "dziko lapansi ndi okhalamo alambire" monga mwa ziphunzitso za umunthu osati pakutsatira Mau a Mulungu. Lero ziphunzitso zomwe sizikupezeka m'Mabukhu Oyera za mpingo wa Aroma zikuphunzitsidwa pafupifupi m'mipingo yonse ya chikhristu, ndi zipembedzo zina za dziko lapansi.

Yesu anati, "...andilambira Ine kwachabe, ndikuphunzitsa maphunzitso malangizo a anthu." Injeel Marko 7:7.

Zina za ziphunzitso zolakwika zomwe zafalikira pa dziko lonse ndi izi:

Mulungu alibe sasamala chomwe munthu amadya. Palibe kusiyana nyama zoyeretsedwa (*hallel*) ndi zodetsedwa (*haram*).

Nyama ya nkhumba ikudyedwa popanda choletsa. Tchimoli ladzetsa matenda osaneneka. Mabuku Oyera akufotokoza momveka kuti nyama zina siziyenera kudyedwa ngakhale kuzikhuza kumene. Ndondomeko ya nyama zomwe Mulungu anati ndi zodetsedwa (*haram*) ikupezeka



m'Chipangano Chakale Taurat Leviticus mutu wa 11. Mwachidule nyama zodetsedwazo (*haram*) ndi ngamila ndi zina zonse za miyendo inai zomwe sizibzikula komanso zosagawanika ziboda, mbira, kalulu, ndi mbewa; nkhumba/nguluwe; nsomba zopanda zipsepse ndi mamba; mbalame zomwe zimadya nyama zinzao. Ndi mpingo wa Aroma ndi ziwalo zake womwe sutha kulekanitsa pakati pa nyama zoyeretsedwa ndi zodetsedwa.

Mpingo wa Aroma'wu umaphunzitsanso kuti zoledzeretsa zidzimwedwa popanda choletsa. Ndipo m'mautumiki ake akupembedza, monga m'utumiki wa "Misa" ansembe amamwa vinyo wosasa, woledzeretsa. Zonsezi Mulungu analetsa, koma chidzudzulo chake sichikumveka ndi mpingo wochita zinthu mwadalawu. Mau a Mulungu akufotokoza momveka bwino:

"Vinyo achita chipwete, chakumwa chaukali chisokosa; wosokera nazo alibe nzeru." Miy. 20:1.

Chiphunzitso china ndi chakumpembedza Mariya amai wa Isa, pompatsa ulemu woyenera Mulungu. Iye akupempheredwa ndi kufunsidwa kuwachitira anthu chifundo ali m'chifanizo cha fano. Mulungu akuletsa zotumikira milungu ina:

"Usakhale nayo milungu ina koma Ine ndekha." Taurat Eks. 20:3.

Ngakhale Mariya anamwalira kale ndipo akupumula m'manda ake, kusamvetsetsa za iye kukupitirirabe. Anthu akumpembedza ati chifukwa amawaonekera "m'masomphenya," lomwe ndi chenjrero la ziwanda, zomwe zimaonekera ngati Mariyayo nkulankhula ndi anthuwo. Ichi ndi chinyengo chachikuru ndi chosokeretsa cha mizimu ya Satana.

"Pakuti ali mizimu ya ziwanda zakuchita zizindikilo..." Chibv. 16:14.

Chiphunzitso china ndi chakusinthidwa kwa lamulo lakupumula pa tsiku lopatulika la chisanu ndi chiwiri la mulungu... la Sabt, Sabata, Saturday...kukhala Sunday, tsiku lopembedza mulungu wa dzuwa. Potsutsa ichi Mulungu anati:

"Muzisunga masabata anga ndithu; pakuti ndiwo chizindikilo pakati pa Ine ndi inu mwa mibadwo yanu; kuti mudziwe kuti Ine ndine Yehova wakukupatulani. Ndipo muzisunga Sabata; popeza ndilo lopatulika la kwa inu....Agwire ntchito masiku asanu ndi limodzi, koma **lachisanu ndi chiwiri ndilo Sabata lakupumula, lopatulika la Yehova....**" Taurat Eksodo 31:13-17.

Ndi zomvetsa chisoni bwanji, kuti pafupifupi dziko lonse, limapumula ku ntchito zake pa Sunday, tsiku loyamba la pa mulungu! Sabata loona likutechdwa la Ayuda, chikhalirecho lamulo la Sabata linakhalako mtundu wa Ayuda usanakhale.

Chinyengo china ndi chogwiritsa ntchito mafano osema a mitengo, miyala, siliva ndi golide kwa mipingo yambiri ponena kuti zimathandizira kuti choonadi chidzimveka bwino. Uku ndikuukira Mulungu potsutsana ndi lamulo lake lachiwiri:

"Usadzipangire iwe wekha fano losema, kapena chifaniziro chiri chonse cha zinthu za m'thambo la kumwamba, kapena za m'dziko lapansi, kapena za m'madzi a pansi pa dziko; **usazipembedzere izo, usazitumikire izo;** chifukwa Ine Yehova Mulungu wako ndiri Mulungu wansanje, wakulanga ana chifukwa cha atate ao, kufikira mbadwo wachitatu ndi wachinai wa iwo amene akudana ndi Ine; ndi kuwachitira chifundo anthu zikwizikwi a iwo amene akondana ndi Ine, nasunga malamulo anga." Taurat Eks. 20:4-6.

Kupanga mafano ndikuwagwiritsa ntchito ngati njira imodzi yopembedzera Mulungu ndi tchimo lalikuru.

## CHIPHUNZITSO CHONAMA ZA IMFA

Chiphunzitso china chosokeretsa ndi kutsogolera anthu ambiri kuchiononongeko ndi chakuti munthu akafa ndi kuikidwa m'manda, walowa moyo wina. Ichi chapangitsa anthu ochuruka kukhulupirira kuti angathe kulankhulana kapena kuchitira zinthu limodzi ndi akufa, komwe nkunama. Za akaufa Baibulo limati, "**akufa" kuphatikiza Maryamu "sadziwa kanthu bi."**

"Pakuti amoyo adziwa kuti tidzafa; koma akufa sadziwa kanthu bi, salandira mphotho; pakuti angoiwalika. Chikondi chao ndi mdano wao ndi dumbo lao lomwe zatha tsopano; ndipo nthawi yamuyaya sagawa konse kanthu kali konse kachitidwa pansi pano." Taurat Mlal. 9:5-6.

Ngati akufa samadziwa kali konse, ndi chifukwa ninji kumaganiza kuti amoyo amalumikizana nao? Mau a Mulungu amati akufa amagona tulo osadziwa kanthu, ndipo adzatero mpaka tsiku lamdzukilo. Mabuku Oyera akutsimikiziranso ichi:

"Akufa salemekeza Yehova, kapena ali yense wakutsikira kuli chete." Taurat Mas. 115:17. NIV.

"Chiri chonse dzanja lako lichipeza kuchichita, uchichite ndi mphamvu yako; pakuti mulibe ntchito ngakhale kulingilira ngakhale kudziwa, ngakhale nzeru, kumanda ulikupitako." Taurat Mlaliki 9:10 NLT.

"Ndipo pamene iwo adzati kwa iwe, Funa kwa olaula, ndi obwebweta, amene alira pyepye, nang'ung'udza; kodi anthu sadzafuna kwa Mulungu wao? Chifukwa cha amoyo, kodi adzafuna kwa akufa?" Taurat Yes. 8:19 NLT.

Kumapeto kwa nthawi, kudzakhala kuuka kwa akufa; omwalira onse adzakhala m'manda mwao kufikira panthawiyo.

"Momweno munthu agona pansi, osaukanso; kufikira miyamba kulibe, sadzaukanso, kapena kuukitsidwa pa tulo take. Ha! Mukadandibisa kumanda, mukadandisunga m'tseri, mpaka wapita mkwiyo wanu. Mukadandiikira nthawi, ndi kundikumbukira. Atafa munthu, adzakhalanso ndi moyo kodi? Ndi kadayembekeza masiku onse a nkhondo yanga, mpaka kwafika kusandulika kwanga. **Mukadaitana, ndipo ndikadakuyankhani**; mukadakhumba ntchito ya manja anu." Taurat Yobu 14:12-15.

"Akufa anu adzakhala ndi moyo; mitembo yao idzauka. Ukani muyimbe, inu amene mukhala m'pfumbi!" Yes. 26:19.

"Taonani, ndikuuzani chinsinsi; sitidzagona tonse, koma tonse tidzasandulika, mkamphindi, m'kutwanima kwa diso, pa lipenga lotsiriza; pakuti lipenga lidzalira, ndipo akufa adzaukitsidwa osabvunda, ndipo ife tidzasandulika. Pakuti chobvunda ichi chiyenera kudzabvala chisabvundi ndi chakufa ichi kubvala chosafa." 1 Akor. 15:51-53."

Ndi ziphunzitso zochepa tawerengazi, zikuoneka kuti Satana, wamwetsa anthu "vinyo" [ziphunzitso] woledzeretsa wa Babulo, ndi cholinga chosokeretsa malingaliro komanso kumvera ndi kudalira kwao pa Mulungu. Mabuku Oyera sakuwerengedwanso ndipo ziphunzitso ndi malingaliro za umunthu ndizo zikukwezedwa. Ha! Satana akulinamiza bwanji dziko lonse lapansi! Ndi anthu ochepa bwanji omwe akuzindikira kuti akutsatira ziphunzitso za uchimo zotsogolera kuchiononongeko!

## MNGELO WACHITATU: NGATI WINA ALAMBIRA CHIROMBO NDI FANO LAKE...

Pomwe tikupitiriza kuphunzira za ziweruziro zochititsa mantha ngati momwe zinaperekedwerapo m'nthawi ya Nowa chigumula chachikuru chija chisanafike, tapeza kuti Chibvumbulutso chimene Allah anapatsa kwa Yesu nichilembedwa ndi Yahaya ku m'mibadwo ya mtsogolo ino, muli chenjezo lalikuru lomwe silinayambe lapaerekedwapo ku mtundu wa anthu. Mu uthenga wa mngelo wachitatu wapatsidwawo kwa ife ndi kwa anthu onse muli chenjezo za chiweruzo cha Mulungu ndi kuopsya kwakulandira "Chizindikiro cha chirombo" m'masiku otsiriza ano.

"Ndipo anawatsata mngelo wina, wachitatu, nanena ndi mau akuru, Ngati wina alambira chirombocho, ndi

fano lake, nalandira lemba pamphumi pake, kapena pa dzanja lake, iyenso adzamwako ku vinyo wa mkwiyo wa Mulungu, wokonzeka wosasanganiza m'chikho cha mkwiyo wake; ndipo adzazunzika ndi moto ndi sulfure pamaso pa angelo oyera mtima ndi pamaso pa Mwanawankhosa." Injeel Chibvumbulutso 14:9-10.

Nanga mau akuti "kulambira chirombo" akutanthauzanji? Nanga kulandira "chizindikilo" pamphumi kapena pa dzanja, zikuimira chiyani? Nanga "vinyo wa mkwiyo" wa Mulungu ndi chiyani? Tipeza mayankho a mafunso'wa m'masamba otsatirawa. Tisanayambe zonse, tisaiwale pemphero (*du'a*) kwa Mulungu kuti atithanzize kupeza mayankho oyenerera a mafunsowa. Iye ndi wolora kutithandiza kumvetsetsa izi monga anachitira pompatsa nzeru Danieli, zakumvetsetsa masomphenya a maulosi kale.

"**Ndaturuka [ndadza] tsopano ine kudzakuzindikiritsa...; zindikira tsopano mau awa,** nulingirire masomphenyawo." "**Dziwa tsopano, nuzindikire**..." Taurat Danieli 9:22, 23, 25.

Monga Mulungu anapatsa chidziwitso kwa Danieli, angathenso kutipatsa ife luntha lakumvetsetsa maulosi a m'Chibvumbulutso. Bukhu'lo likutifokozera kuti,

"Ndipo dziko lonse linazizwa" ndi chinachitikacho [chakuti chirombo chinapatsidwanso ulamuliro] ndipo anthu analambira [kutsatira] chirombo." Injeel Chibvumbulutso 13:3 NLT.

Kunena motsindika chirombo ndi atumiki ake chidzayesetsa kukhazikitsa ulamuliro wake pa dziko lonse. Koma ndi anthu okhawo amene sadzalandira "chizindikilo" cha chirombo'cho adzachilaka.

"Ndipo anachipatsa icho kuchita nkhondo ndi oyera mtima, ndi kuwalaka; ndipo anachipatsa ulamuliro wa pa pfuko liri lonse, ndi anthu, ndi manenedwe, ndi mitundu. Ndipo adzachilambira onse akukhala padziko, amene dzina lao silinalembedwa m'bukhu la moyo la Mwanawankhosa, wophedwa kuyambira makhazikidwe a dziko lapansi." Chibvumbulutso 13:7-8.

Kumapeto kwa zonse kudzakhazikitsidwa lamulo lakuti munthu asaloledwe kugula kapena kugulitsa kupatula okhawo adzakhale nacho "chizindikilo" cha chirombo pamphumi pao ndi pa dzanja lao:

"Ndi kuti **munthu sangakhoze kugula kapena kugulitsa,** koma iye yekha wakukhala nacho chilembo [chizindikilo] ndilo dzina la chirombo, kapena chiwerengero cha dzina lake. Chibvumbulutso 13:17.

Umu ndimo chirombo chidzayesetsere kudzitengera mwa icho chokha ulamuliro wa dziko lonse lapansi, poyamba mwa chinyengo ndi machitidwe a zozizwa, kenaka m'machitidwe a za chuma, potsirizira pakuopsyeza ndi chilango cha imfa.

"...onse osalambira fano la chirombo aphedwe." Chibvumbulutso 13:15.

## CHIROMBO: KODI NDI NDANI?

Tisanapitirize kufotokoza za "kupembedza chirombo," timvetse chomwe liu chirombo likuimira ndi yemwe ali chrombocho. Mu ulosi "chirombo" ndi mtundu wa anthu kapena ulamuliro wa dziko lapansi. Tinayamba kumva za ulamuliro wa chirombo kuchokera m'bukhu la Danieli pa mutu wa "nyanga yaing'ono." Danieli 7:8; 8:9. "Nyanga Yaing'ono" ndi ulamuliro womwe "unayesa kusintha nthawizo ndi chilamulo [zoikidwa ndi Mulungu]." Danieli 7:25.

M'Chibvumbulutso cha Yesu tikuwerengamo kuti ulamuliro umenewu ukufotokozedwanso kuti uli chirombo – chirombo cha maonekedwe a chokhachokhao! Pa Chibvumbulutso 13:1-2. Ukufotokozedwa kuti:

"Ndipo ndinaimirira pa mcenga wa nyanja. Ndipo ndianona chirombo chirinkuturuka m'nyanja, chakukhala nazo nyanga khumi, ndi mitu isanu ndi iwiri, ndi pa nyanga zake nduwira za chifumu khumi, ndi pamitu pake maina a mwano. Ndipo chirombo ndinachionacho chinafanana ndi nyalugwe, ndi mapazi ake ngati mapzi afisi, ndi pakamwa pake ngati pakamwa pa mkango; ndipo chinjoka chinampatsa iye mphamvu yake, ndi mpando wachifumu wake, ndi ulamuliro waukuru."

Timvetsetsetu! Malemba akuti si Mulungu amene anapatsa ulamuliro ndi mphamvu yake kwa chirombo, koma [Satana].

"Chirombo" kapena ulamuliro ukufotokozedwa'wu ndi Upapa wa Aroma. Upapa ndiwo ukutsogolera mchitidwe wa chipembedzo womwe pachiyambi unali woyera, koma m'kupita kwa nthawi unalowerera ndikusakanikira m'machitidwe a chikunja, polora ziphunzitso ndi machitidwe achikunja m'kapembedzedwe, ziphunzitso ndi chikhulupiriro zake. Umakweza kwambiri miyambo ndi malamulo a mpingo ndi kunyalanyaza malamulo a Mulungu. Uwu ndi mchitidwe wa chipembedzo chopandukira Mulungu womwe wafalikira pa dziko lapansi. M'Mabuku Oyera akuufotokoza kakhumi ndi kawiri kuti uli:

"nyanga yaing'ono" Danieli 7 ndi 8.

"munthu wakusayeruzika" 2 Atesalonika 2:3.

"mfumu ya nkhope yaukali" Danieli 8:23.

"mkazi wobvala chibakuwa" Chibvumbulutso 17:4.

"mkazi wachigololo" Chibvumbulutso 17:1; 19:2.

"chirombo" Chibvumbulutso 13-17; 19:20.

"666" Chibvumbulutso 13:18.

"Babulo Waukuru" Chibvumbulutso 17:5; 18:2.

"amai wa achigololo" Chibvumbulutso 17:5

"chinsinsi cha kusayeruzika" 2 Atesalonika 2:7.

"wa zonyansa za dziko" Chibvumbulutso 17:5.

"wokana Yesu" 2 Yohane 2:22; 4:3.

Kufuna kupembedzedwa ndi chilakolako cha Satana, ndipo mu mchitidwe wa uzimu wabodzawu iye akupembedzedwa ndi anthu a dziko lapansi. Amamva kulemekezedwa anthu akamapereka ulemu ku mchitidwe wa Upapa polilemekeza Sunday kuposa pompatsa ulemu Mulungu polilemekeza tsiku limene Mulungu'yo anapumula ndi kulipatula la chisanu ndi chiwiri.

## TSIKU LA SABATA LAKUPUMULA

M'munsimu ndi mbiri mwa chidule ya kulengedwa kwa dziko ndi Mpumulo [Sabata] wa Mulungu:

"Tsiku lachisanu ndi chiwiri Mulungu anamariza ntchito yonse anaipanga; ndipo anapuma tsiku lachisanu ndi chiwiri ku ntchito yake yonse. Mulungu ndipo anadalitsa tsiku lachisanu ndi chiwiri, naliyeretsa limenelo." Taurat Genesis 2:2-3.

Kwa anthu akale omwe kunapatsidwa choonadi cha Mau a Mulungu'chi kunapatsidwanso mphamvu ya "... **kuchiphunzitsa ichi momveka bwino ku mtundu wonse wa anthu osabisa kanthu kali konse za icho; koma iwo ananyalanyaza nachipondereza ichi,** pakutero anadzitengera okha temberero! Ndipo kusayeruzika kunakhala chopindula chao!." Sura 3:187 Aal-E-Imram.

Mau a m'Baibulo anaperekedwa kuti "aphunzitsidwe" kwa anthu, zachisoni! Bungwe lina la za chipembedzo layesetsa kusintha malamulo a Mulungu. Laika "miyambo" yaumunthu, kuphatikiza Sunday lachikunja m'malo mwa Sabata loona.

## ULOSI WA USA M'BUKHU LOPATULIKA

"Ndipo ndinaona chirombo china chirikuturuka pansi; **ndipo chinali nazo nyanga ziwiri ngati za mwana wa nkhosa**, **ndipo chinalankhula ngati**



**chinjoka**. Ndipo chichita ulamuliro wonse wa chirombo choyamba pamaso pake. Ndipo chilambiritsa dziko ndi iwo akukhala momwemo chirombo choyamba, chimene bala lake la ku imfa lidapola.

"Ndipo chichita zizindikilo zazikuru, kutinso chitsitse moto uchokere m'mwamba nugwe pa dziko, pamaso pa anthu. Ndipo chisokeretsa iwo akukhala padziko ndi zizindikilo zimene anachipatsa mphamvu yakuzichita pamaso pa chirombo, ndi kunena kwa iwo akukhala padziko, kuti apange fano la chorombocho, chimene chinali nalo bala la lupanga nichinakhalanso ndi moyo.

"Ndipo anachipatsa mphamvu yakupatsa fano la chirombo mpweya, kutinso fano la chirombo lilankhule, nilichite kuti onse osalilambira fano la chirombo aphedwe. Ndipo chichita kuti onse, ang'ono ndi akuru, achuma ndi osauka, ndi mfulu ndi akapolo, alandire chilembo pa dzanja ndi pamphumi pao; ndi kuti munthu sangakhoze kugula kapena kugulitsa, koma iye yekha wakukhala nacho chilembo, ndilo dzina la chirombo, kapena chiwerengero cha dzina lake. Pano pali nzeru. Iye wakukhala nacho chidziwitso awerenge chiwerengero cha chirombocho; pakuti chiwerengero chake ndi cha munthu; ndipo chiwerengero chake ndicho mazana asanu ndi limodzi mphambu makumi asnu ndi limodzi kudza zisanu ndi chimodzi." Chibv. 13:11-18 KJV.

Chirombo chachiwiri choturuka pansi cha Chibvumbulutso 13 chikulimbikitsa ziphunzitso zolakwika za Aroma; chiri mtumiki wamkuru wokakamiza sabata la Sunday kuyambira m'dziko lomwe chikulamulira kufikira dziko lonse lapansi. Poyamba chirombo cha ngati nkhosachi chinali ngati cha Chikhristu, koma kumatsiriziro a nthawi kuno chikulankhula ngati chinjoka – Satana. Kutanthauza kuukira Mulungu kwa USA ndi mipingo yake ya Mpanduko (Protestantism)

Kuukiraku kukuchitika kudzera m'malamulo okhazikitsidwa ndi mabungwe ndiponso misonkhano

yoikika m'dzikolo, mogwirizana ndi atsogoleri akugwa a za chipembedzo, omwe ali mkati kukhazikitsa malamulo otsutsana ndi a Mulungu.

## DZKO LAFIKA M'ORA LAKE LOTSIRIZA

Muyeso wa kuipa kwa okhala pa dziko wafika poyamba kusefukira. Dziko lafika pakuti Mulungu angolisiya ndi kulora Satana kuliononga monga akufunira. **Kukweza kwa malamulo a anthu m'malo mwa malamulo a Mulungu, kugwiritsa ntchito mphamvu ya umunthu, komanso kukwezedwa kwa Sunday, m'malo mwa Sabata la m'Mabuku Oyera, ndi zochitika zotsiriza. Kuchotsedwa kwa malamulo akeku kukakwanira dziko lonse, pomwepo Mulungu adzazibvumbulutsa m'chilungamo.** Iye adzauka mu mphamvu yake, kuligwedeza dziko kolimba. Iye adzaturukira kuchokera m'malo ake oyera kudzalanga oipa okhala pa dziko chifukwa cha kuipa kwao, ndipo dziko lidzapereka mwazi wake, osatha kubisanso akufa ake.

Tafika ife mu nthawi zowawitsa, osati ku ntchito za chuma ndi chikhalidwe zokha, komanso ku moyo wathu wa uzimu. Tibwerere kwa Mulungu, kumvera ndi kuchita zomwe Malemba ake Oyera akunena. Kusankha ziphunzitso zogarukira Mulungu za Aroma ndi za mipingo yakugwa ya Mpanduko ndi kukana ziphunzitso za Mulungu, ndi kupanda nzeru ndipo chotsatira chake chidzakhala chilango cha imfa.

Bukhu Lopatulika likutsimikiza kuti anthu onse amene adzalandira chizindikilo cha chirombo adzalangidwa. Awa ndi omwe anasinthanitsa malamulo a Mulungu ndi malamulo a anthu.

"Iyenso [wokweza Sunday ndi umunthu] adzamwako ku vinyo wa mkwiyo wa Mulungu, wokonzeka wosasanganiza m'chikho cha mkwiyo wake; ndipo adzazunzika ndi moto ndi sulfure pamaso pa angelo oyera mtima ndi pamaso pa Mwanawankhosa." Chibv. 14:10.

Koran Wolemekezeka akuchenjezanso Anthu a Bukhu:

"Akadakhala kuti Anthu a Bukhu anakhulupirira ndi kukhala olungama, Mosakaika konse tikanawakhululukira zosalungama zao ndi kuwalandira iwo m'minda ya madalitso." Sura 5:65 Al-Maeda.

"Kukanakhala kuti" iwo anamvera Bukhu ndi kuchita chifuniro cha Mulungu... Koma iwo anayesera kusintha chilamulo choyeracho. Mkwiyo wa Mulungu ugwera onse amene akulimbikitsa kusintha Malamulo ake kosabvomerezekako.

"Lankhula nunene: 'Ha, Anthu a Bukhu! Simungakhale ndi maziko akuti nkukhazikikapo, pokhapokhapo mugwiritse Malamulo, Uthenga Wabwino ndi mabvumbulutso anapatsidwawo ndi Mulungu kwa inu..." Sura 5:68 Al-Maeda.

## MOMWE TINGAPEWERE CHIZINDIKILO CHA CHIROMBO

Timvere malamulo oyera a Mulungu omwe ali m'Chipangano chake, ndipo anapatsidwa kwa Mussa pansonga za phiri la Sinai.

"Ndipo Ife tinapereka malamulo okhuza zinthu osiyanasiyana kwa Mussa, olembedwa pa magome a miyala, olamulira ndi kufotokoza za zinthu zonse (tinamuuza): '**Landira ndi kuwasunga awa mokhulupirika,** ndi kuwaphunzitsanso anthu ako, awasungitse ndi kukhala mosamalitsa m'menemo..." Sura 7:145 Al-Araf.

Lero Mulungu akufunsa anthu onse funso lomwe anamfunsanso Mussa kale:

"Mukana kusunga zouza zanga ndi malamulo anga kufikira liti?" Taurat Eksodo 16:28.

Njira yokhayo yoongoka ndiyo kumvera ndi kusunga malamulo onse a Mulungu kuphatikiza la chinai la mpumulo wa tsiku la Sabata loyera. Chipangano cha Mulungu cholembedwa pa magome a miyala, chinapatsidwa kwa olengedwa onse kuti asunge malamulo ndi maweruzo ake oyera ku nthawi zonse.

"Potero muwasunge malamulo anga, ndi kuwachita; Ine ndine Yehova." Taurat Lev. 22:31.

"...pakumvera inu mau a Yehova Mulungu wanu, **kusunga malamulo ake** onse amene ndikuuzani lero lino, kuchita zoyenera pamaso pa Yehova Mulungu wanu." Taurat Deut. 13:18.

Njira yokhayo mitima yathu ingakhale pa chiyanjano ndi Mulungu ndiyo kuyenda m'malamulo ake onse.

"Mitima yanu ikhale yangwiro ndi Yehova Mulungu wathu, kuyenda m'malemba ake ndi kusunga malamulo ake monga lero lino." Taurat 1 Maf. 8:61.

"Mau atha, zonse zamveka zatha; opa Mulungu nusunge malamulo ake; pakuti choyenera anthu onse ndi ichi." Taurat Mlaliki 12:13.

Kodi Mulungu amasunga pangano lake ndi yani?

"...Ambuye Mulungu wamkuru ndi woopsa, wakusungira pangano ndi chifundo iwo akukukondani, ndi kusunga malamulo anu..." Taurat Dan. 9:4.TNIV

Isa Mpulumutsi mwana wa Maryamu anatiphunzitsa:

"...koma ngati ufuna kulowa m'moyo, **sunga malamulo**." Injeel Mat. 19:17.

"Pakuti ichi ndi chikondi cha Mulungu, kuti tisunge malamulo ake: ndipo malamulo ake sali olemetsa."Injee1 Yoh. 5:3.

## KODI ANTHU OCHIMWA ANGATHE KUSUNGA MALAMULO OYERA A ALLAH?

Tikadzipereka ku chifuniro cha Mulungu ndi Isa Mpulumutsi, amene anatumidwa kuchokera kumwamba, tidzalandira mphamvu yotilimbikitsa kuchita chifuniro chake nthawi zonse. "...akuyeseni inu opanda chirema m'chinthu chiri chonse chabwino, kuti muchite chifuniro chake; ndi kuchita mwa ife chokondweretsa pamaso pake, mwa Yesu Khristu, kwa Iyeyu ukhale ulemelero ku nthawi za nthawi." Ahebri 13:12 LITV.

Kodi Mulungu angakwaniritse kutikonzanso motani? Iye analonjeza kuchita chinthu chiri chonse mwa ife chimene ife eni sitingathe kudzichitira . Tikhale ndi Mzimu wa Mulungu kuti Iye achite ntchito yokonza miyoyo yathu. Tikadzikhuthula kwa Iye, Iye adzakwaniritsa chifuniro chake mwa ife. Tikamfunitsitsa, Mulungu adzalemba lamulo lake loyera m'mitima ndi m'malingaliro athu ndipo tidzachirimika pakumvera ndi kulichita ili nthawi zonse. Tidzasunga chilamulo chake choyeracho.

"Koma ili ndi pangano langa limene ndidzapangana ndi nyumba ya Israyeli atapita masiku aja, ati Yehova; ndidzaika chilamulo changa m'kati mwao, ndipo m'mitima mwao ndidzachilemba; ndipo ndidzakhala Mulungu wao, nadzakhala iwo anthu anga." Taurat Yeremiya 31:33.

Uthenga Wabwino, ukufotokoza momwe Mulungu angakonzere miyoyo ya onse omlora kutero. Kale, Mulungu analemba malamulo ake pa magome a miyala, koma m'masiku otsiriza ano, Iye adzalonga awa m'mitima ndi m'malingaliro athu.

"Ichi ndi chipangano ndidzapangana nao, atapita masiku ajawo, anena Ambuye, **Ndidzapereka malamulo anga akhale pamtima pao; ndipo pa nzeru zao ndidzawalemba**...." Ahebri 10:16.

Koma anthu a dziko lapansi watangwanika kupondereza malamulo a Mulungu.

Ndi pemhero (*dua*) lathu kuti awerengi onse a zolemberazi apereke mitima ndi malingaliro ao kwa Mulungu kuti Iye alembe malamulo opatsa ungwiro m'malingaliro ndi m'nzeru zao.

## ANTHU A BUKHU [AKHRISTU] NDI CHIPANGANO

"Kumbukirani kuti Mulungu anachotsa chipangano chake kwa Anthu a Bukhu [Akhristu], ndi kuchizindikiritsa ichi



momveka bwino kwa anthu amitundu ina, kuti iwo asachibise ichi: **koma iwo anachipondereza osachisamalira,** pakutero anadzitengra okha phindu la themberero! Ndipo kuipa ndi phindu lomwe iwo analipanga!" Sura 3:187 Aal-E-Imran.

Kodi mau awa anakwanitsidwa bwanji m'mbuyomu? Pansi pa ulamuliro wa Upapa wa Mpingo wa Aroma wa dziko lonse, atsogoleri ake analetsa:

"Kuwerenga Bukhu Lopatulika, kumvetsera kapena kulilalikira, kapena kungolankhula zokhuzana nalo, kungotero chilango chake chinali kuponyedwa pamoto munthu ali moyo. Kupemphera Mulungu m'malo a mseri, kukana kugwadira zinthunzi [mafano], kuyimba Masalmo, zonsezo chilango chake chinali imfa." *The Great Controversy,* p. 240.

Podzikundikira mphamvu zochuruka, atsogoleri a Mpingo wa Katolika analamulira mafumu ndi anthu wamba m'Zaka Za Mdima [Dark Ages].

"...Kwa zaka mazana Bukhu Lopatulika linali loletsedwa. Anthu anakanizidwa kuliwerenga ngakhale kukhala nalo m'nyumba zao, ndipo ansembe osowa khalidwe osaopa Mulungu anamasulira ziphunzitso za Baibulo modzichinjiriza okha. Kutero kunapangitsa kuti Papa yemwe pafupifupi dziko lonse linamgwadira, afike podzimva kuti ali nthumwi ya Mulungu pa dziko lapansi, nadzitengera ulamuliro wa zachipembedzo ndi dziko." Ibid.. p.51.

Umu ndimo Baibulo kapena, "muyeso wakulekanitsa chabwino ndi choipa" monga limatchulidwira m'Koran Lolemekezeka, linapeputsidwira ndi kusasamalidwa.

"Kale tinatumiza amithenga athu ndi Zizindikiritso Zomveka bwino. Tinatumiza iwo ndi Bukhu, **Muyeso**

(Wolekanitsa Chabwino ndi Choipa), kuti anthu ayende m'chilungamo …" Sura 57:25 Al-Hadid.

Mukukumbuka chomwe chinapatsidwa kwa Mussa m'chipululu?

"Ndipo kumbukirani, Ife tinampatsa Mose Malambo ndi Maweruzo Olekanitsa (chabwino ndi choipa): Kupereka mwai kwa inu wakutsogoledwa m'chilungamo." Sura 2:53 Al-Baqara.

Koma Aroma pansi pa upapa anayesetsa kufafaniza Malembo ndi "Maweruzo" olekanitsa chabwino ndi choipawo. Iwo ayesetsa kusintha mau ndi malamulo ena a m'Baibulo ndi kuwatanthauzira molakwika.

## KODI MAU A ALLAH AKALEKALEWO ANASINTHIDWA?

"Koma opandukirawo **anasintha mauwo** kuwachotsa m'choonadi monga chinaperekedwera pachiyambi kwa iwo: Ndipo Ife tinatumiza pa



opulukirawo chilango kuchokera kumwamba, chifukwa **iwo anasemphanitsa (maweruzo) athu mobwerezabwereza**." Sura 2:59 Al-Baqara.

Aneneri akale analoserapo za kusakaniza choonadi ndi chikunjaku. Danieli anati uzadza ulamuliro womwe udzayesetsa kusintha Malamulo ndi Mau a Mulungu:

"Nidzanena [nyanga yaing'ono/ ulamuliro wa upapa] mau akutsutsana ndi Wam'mwambamwamba, nidzayesa kusintha nthawizo ndi chilamulo.." Danieli 7:25.

Yesaya wa patsogolo pa Danieli, ananeneraponso:

"Dzikonso laipitsidwa ndi okhalamo ake omwe, chifukwa iwo alakwa pamalamulo **nasinthanitsa malemba; nathyola chipangano cha nthawi zonse**." Yesaya 24:5 NLT.

Baibulo la King James likutinso:

"Dzikonso laipitsidwa ndi okhalamo ake; chifukwa iwo **alakwira pa malamulo, asinthanitsa malemba, nathyola chipangano chosatha**." Yesaya 24:5 KJV.

N'chiyani chinasinthidwa m'Mau a Mulungu?

Malamulo Khumi, malemba ndi maweruzo ena a Mulungu ndizo zinasinthidwa.

Nanga malamulo a Mulungu'wa "**anasinthidwa**" (Sura 2:59 Al-Baqara) motani? Malamulowa anasinthidwira motere:

Mpingo wa Aroma unalamulira kulilemekeza Sunday, tsiku lopembedza mulungu wachikunja wa dzuwa, m'malo mwa la Sabata (As-Sabt) loyera la Mulungu.

Zakudya monga nkhumba (nguluwe), ndi nyama zina zodetsedwa (*haram*) sizikukhala ngati zodetsedwa.

Mafano osema akugwiritsidwa ntchito m'mautumiki akupembedza mu mpingo wa Aroma/ wa Upapa.

Masewera a njuga ndi zakumwa zoledzeretsa zomwe zikuletsedwa m'Bukhu Lopatulika, zikuchitidwa popanda choletsa ndi anthu ochuruka odzichawo akhristu. Ansembe amagwiritsa ntchito zoledzeretsa pa Misa/Ukaristia.

Mariya kupempheredwa ngati Mulungu. Ndani akuphunzitsa akhristu kupembedza Maryamu? Sura 5:115 Al-Maeda. Si Yesu Mpulumutsi, koma atsogoleri opembedza mafano a chi-Roma/upapa opandukira Mulungu.

"Inu Anthu a Bukhu! chifukwa chiyani mukutchingira chooandi m'chisalangamo, ndi kuchipondereza Choonadi, chikhalirecho mukuzindikira?" Sura 3:71 Aal-E-Imran.

Anthu onse apa dziko akuuzidwa abwerere kukumvera Malamulo a Mulungu omwe ali chikhalire oyera monga anali pachiyambi pomwe amaperekedwa kumtundu wa anthu. Malamulo'wa anayamba kunyalanyazidwa ndi Israyeli wakale nthawi ya ukapolo wao m'Aigupto. Atapulumutsidwa, Mulungu anakumbutsa Mussa ndi ana a Israyeli zakufunikira kwa malamulo oyerawa. Mussa anaitanidwa ku nsonga zazitali za phiri la Sinai, kukapatsidwa Malamulowo pa magome a miyala olembedwapo ndi Mulungu mwini, kuti munthu athe kudziwerengera yekha.

**Posachedwapa lamulo la Sunday likakamizidwa pa dziko lonse.**

"Ndipo chirombo {cha ngati mwana wa nkhosa - USA] chichita kuti onse, ang'ono ndi akuru, achuma ndi osauka. Ndi mfulu ndi akapolo, alandire chilembo pa dzanja lao ndi pamphumi pao; ndi kuti munthu sakhoza kugula kapena kugulitsa, koma iye yekha wakukhala nacho chilembo, ndilo dzina la chirombo, kapena chiwerengero cha dzina lake." Chibvumbulutso 13:16-17.

Okondedwa, kumvera malamulo olemekeza Sunday, ndiko kulandira "chilembo [chizindikilo]" chogarukira Mulungu. Ndikusonyeza [kuchita] "chilembo cha chirombo/upapa."

Ndani alandire chilembo cha chirombo? Ndani achikane? Ndani adzachirimika pachikhulupiriro chake pa Mulungu ndi Malamulo ake oyera? Ndani adzatchinjiriza choonadi, pamene anthu omzungulira adzakhale achikana? Mudzaima inu?

## MALAMULO A MULUNGU: TAURAT

Iyi ndi ndondomeko ya Malamulo a Mulungu yomwe ikupezeka 'Chipangano Chakale [Taurat]:

I. "Usakahale nayo milungu ina koma Ine ndekha.

II. "Usadzipangire iwe wekha fano losema, kapena chifaniziro chiri chonse cha zinthu za m'thambo la kumwamba, kapena za m'dziko lapansi, kapena za m'madzi a pansi pa dziko; usazipembedzere izo, usazitumikire izo; chifukwa Ine Yehova Mulungu wako ndiri Mulungu wansanje, wakulanga ana chifukwa cha atate ao, kufikira mbadwo wachitatu ndi wachinai wa iwo amene akudana ndi Ine; ndi kuwachitira chifundo anthu zikwizikwi a iwo amene akondana ndi Ine, nasunga malamuo anga.

III. "Usatchule dzina la Yehova Mulungu wako pachabe; chifukwa Yehova sadzamuyesa iye wosachimwa amene atchula pachabe dzina lakelo.

IV. "Uzikumbukira tsiku la Sabata, likhale lopatulika. Masiku asanu ndi limodzi uzigwira ndi kumariza ntchito zako zonse; koma tsiku lachisanu ndi chiwiri ndilo Sabata la Yehova Mulungu wako; usagwire ntchito iri yonse, kapena iwe wekha, kapena mwana wako wamwamuna, kapena mwana wako wamkazi, kapena wantchito wako wamwamuna, kapena wantchito wako wamkazi, kapena nyama zako, kapena mlendo amene ali m'mudzi mwako; chifukwa masiku asanu ndi limodzi Yehova adamariza zakumwamba ndi zapansi, ndi nyanja, ndi zinthu zonse ziri m'menemo, napumula tsiku lachisanu ndi chiwiri; chifukwa chake Yehova anadalitsa tsiku la Sabata kuti likhale lopatulika.

V. "Uzilemekeza atate wako ndi amako; kuti achuruke masiku ako m'dziko limene Yehova Mulungu wako wakupatsa iwe.

VI."Usaphe.

VII. "Usachite chigololo.

VIII. "Usabe.

IX. "Usamnamizire mnzako.

X. "Usasirire nyumba yake ya mnzako, usasirire, mkazi wake wa mnzako, kapena wantchito wake wamwamuna, kapena wantchito wake wamkazi, kapena ng'ombe yake, kapena buru wake, kapena kanthu kali konse ka mnzako." Taurat Eksodo 20:1-17.

Malamulo Oyera a Mulungu ndi a ku




nthawi zonse, ndi a anthu amitundu yonse ndi a mibadwo yamtsogolo. Mulungu anatsimikiza mtima za awa nalumbira:

"Sindidzaipsa chipangano changa, kapena kusintha mau oturuka m'milomo yanga." Zabur Masalmo 89:34.

## MALAMULO A MULUNGU M'CHIPANGANO CHATSOPANO: INJEEL

Malamulo a Mulungu m'Chipangano Chatsopano/Injeel:

I. "Ambuye Mulungu wako udzamgwadira, ndipo Iye yekha yekha udzamlambira." Mateyu 4:10.

II. "Tiana dzisungeni nokha kupewa mafano." "Popeza tsono tiri mbadwa za Mulungu, sitiyenera kulingalira kuti umulungu uli wofanafana ndi golide, kapena siliva, kapena mwala, wolocha ndi luso ndi zolingalira za anthu." 1 Yohane 5:21; Machitidwe 17:29.

III. "Kuti dzina la Mulungu ndi chiphunzitso zisachitidwe mwano." 1 Timoteo 6:1.

IV. "Ndipo pempherani kuti kuthawa kwanu kusakhale pa nyengo ya chisanu, kapena pa Sabata." "Sabata linaikidwa chifukwa cha munthu, si munthu chifukwa cha Sabata; motero Mwana wa munthu ali mwini dzuwa la Sabata." "Pakuti wanena pena za tsiku lachisanu ndi chiwiri, natero, Ndipo Mulungu anapumula tsiku lachisanu ndi chiwiri, kuleka ntchito zake zonse. "Momwemo utsalira mpumulo wa Sabata wa kwa anthu a Mulungu. Pakuti iye amene adalowa mpumulo wake, adapumulanso mwini wake, ku ntchito zake, monganso Mulungu ku zake za Iye." "Pakuti mwa Iye, zinalengedwa zonse za m'mwamba, ndi za padziko." Mateyu 24:20; Marko 2:27, 26; Ahebri 4:4, 9, 10; Akolose 1:16.

V. "Lemekeza atate wako ndi amako."

Mateyu 19:19.

VI. "Usaphe." Aroma 13:9.

VII. "Usachite chigololo." Mateyu 19:18.

VIII. "Usabe." Aroma 13:9.

IX. "Usamnamizire mnzako". Aroma 13:9.

X. "Usasirire." Aroma 7:7.

"Potero kodi lamulo tiyesa chabe mwachikhulupiriro? Musatero ai; koma tikhazikitsa lamulo." Aroma 3:31. "Ndipo… pa Sabata anapumula monga mwa lamulo." Luka 23:54-56.

Zakusunga Sabata m'dziko likudza'lo: "Pakuti monga m'mwamba mwatsopano ndi dziko lapansi latsopano limene ndidzalenga, lidzakhalabe pamaso pa Ine, ati Yehova, momwemo adzakhalabe ana anu ndi dzina lanu. Ndipo kudzakhala kuti kuyambira pa mwezi wokhala kufikira ku unzake, ndi kuyambira pa Sabata lina kufikira ku linzake, anthu onse adzafika kudzapembedza panaso pa Ine ati Yehova." Yesaya 66:22-23 werenganinso Marko 2:27-28.

## MALAMULO A MULUNGU M'KORAN WOLEMEKEZEKA

"Kumbukira iwe kuti tinakupatsa Chipangano chako pokhala ife pamwamba pako m'phiri (la Sinai). (Ndikunena): Gwiritsa chomwe Ife takupatsacho iwe, ndi kuikpo mtima (pa Chilamulo)." Sura 2:93 Al-Baraqa.

"Ndi Iye amene anakutumizira iwe (pang'ono pang'ono), m'choonadi, Bukhu, kukufotokozera zomwe zinachitika ilo lisanalembedwe." Sura 3:3 Aal-E-Imran.

**1.** "Mulungu walamulira iwe usapembedze milungu ina koma Iye Yekha." Sura 17:23 Al-Isra.

"…Mulungu…Palibe mulungu wina koma Iye…" Sura 35:3 Fatir.

**2.** "…Koma upewe chidetso cha mafano." Al-Hajj 22:30.

"Pakuti iwo anaimika (mafano) kuwayerekeza ndi Mulungu, kusokoneza (anthu) kuti achoke m'Njirayo Yake!…" Sura 14:30 Ibrahim.

**3.** "Maina abwino okoma ndi omwe Mulungu amadziwika nao: choncho uitanire pa Iye pogwiritsa ntchito awa: upewe anthu amene amatchula kosayenera maina Akewo…" Sura 7:180 Al-Araf.

**4.** "…ndi Mulungu, Amene analenga miyamba ndi dziko lapansi m'masiku

# CHENJEZO LOOPSYA LA ALLA

asanu ndi limodzi, Napumula Pampando wake Wachifumu!" Sura 7:54 Al-Araf.

**"…uwatemberere monga Ife tinatemberera onse akuipsa Sabata…"** Sura 4:47 An-Nisa.

**"…Ife tinalamulira iwo: Musaipse Sabata m'njira iri yonse."** Sura 4:154 Al-Baqara.

**5.** "…Ndikuti mukhale achikondi kwa makolo. Kaya ndi m'modzi kapena onse ndi okalamba." Sura 17:23 Al-Isra.

**6.** "…Musachotse moyo, umene Mulungu anaulenga, pokhapokha pa chifukwa choyenera" Sura 6:151 Al-Anaam.

**7.** "Usayende njira yokuyandikiza ku chigololo: pakuti…chiri tchimo…" Sura 17:32 Al Isra.

**8.** "…Kuti iwo sadzaba…" Sura 60:12 Al-Mumtahina.

"Koma ngati wakuba alapa pambuyo pochita chosayeneracho, nasintha iye khalidwelo, Mulungu amatembenukira kwa iye, ndi kumkhululukira." Sura 5:39 Al-Maeda.

**9.** "…Upewe liu liri lonse lonama." Sura 22:30 Al-Hajj.

"Mulungu samatsogolera munthu ali yense…wonama." Sura 40:28 Al-Ghafir.

"Mugwiritse ntchito m'myeso wokwanira bwino mukamayeza zinthu, muyeze ndi choyezera choongoka…" Sura 17:35 Al-Isra.

**10.** "Ndipo musasirire zibvute zitani…" Sura 4:32 An-Nisa.

"… Ife tinapatsa malamulo kwa iye, olembedwa m'magome a miyala okhuza magawo onse, Kuchenjeza ndi kutanthauzira zinthu zonse, (ndi kuti): Tenga awa ndi kuwagwiritsa molimba, ndi kuwaphunzitsa anthu a mtundu kugwiritsa awa pokhazikika mosamalitsa m'malangizo amenewa …" Sura 7:145 Al-Araf.

"Ndipo pambuyo pao [aneneri], Tinatumiza Yesu mwana wa Mariya, kudzachitira umboni za Malamulo omwe analembedwa patsogolo pake: Tinamizira iye Uthenga Wabwino: momwe muli chitsogozo ndi kuunika, ndiponso umboni wa Malamulo omwe anaperekedwa asanabadwe iye: kukhala nyale yotsogolera ndi malangizo kwa anthu akuopa Allah." Sura 5:46 Al-Maeda.

"Momwemonso Ife tinamuonetsa Abrahamu Ulamuliro wa za m'mwamba ndi dziko lapansi kuti iye atsimikizike pa chikhulupiriro." Sura 6:75 Al-Anaam.

Tilemekeze Mulungu "…Amene anapatsa malamulo ndi chitsogozo…" Sura 87:3 Al-Ala.

## MALAMULO A MULUNGU OSINTHIDWA NDI UPAPA

Malamulo a Mulungu monga mwa mpingo wa Aroma [Upapa].

I. "Ine ndi Yehova Mulungu wako, usakhale nayo milungu ina koma Ine ndekha.

**(Lamulo lachiwiri lopezekalo m'Chipangano Chakale [Taurat], Chipangano Chatsopano [Injeel] ndi m'Koran ndipo likuletsa kupembedza mafano osema linachotsedwa m'malamulo a mpingo wa Aroma).**

II. "Usatchule dzina la Yehova Mulungu wako pachabe.

III. "Uzikumbukira kusunga tsiku la Sabata kukhala loyera."

M'bukhu lotchedwa *Doctrinal* [*Catholic*] *Catechism*, page 174, muli funso ndi yankho lakuti,

"FUNSO: Kodi muli ndi chitsimikizo chanji kuti Mpingo [wa Aroma] uli ndi mphamvu yakusintha zikondwerero zoikika ndiponso malamulo?

"YANKHO: Ukadakhala kuti unalibe mphamvu yakutero…mpingo **sukadaika Sunday, tsiku loyamba la pa mulungu, kukhala lolemekezeka, m'malo mwa Saturday, tsiku lachisanu ndi chiwiri, kusintha komwe kulibe ulamuliro wochokera m'Mau a Mulungu.**"

IV. "Uzilemekeza atate wako ndi amako.

V. "Usaphe.

VI. "Usachite chigololo.

VII. "Usabe

VIII. "Usachitire umboni wonama pa mbale wako

IX. "Usasirire mkazi wa mbale wako.

X. "Usasirire katundu wa mbale wako."

*The Convert's Catechism of Catholic Doctrine, p. 50.*

## "NIDZAYESA [NYANGA YAING"ONO] KUSINTHA NTHAWIZO NDI CHILAMULO" DANIELI 7:25.

"…nabvumbulutsike munthu wakusayeruzika…amene atsutsana nazo, nadzikuza pa zonse zochedwa Mulungu, kapena zopembedzeka; kotero kuti iye wakhala pansi ku Kachisi wa Mulungu, nadzionetsera yekha kuti ali Mulungu." 2 Ates. 2:3-4.

Okondedwa, Mabuku Oyera ndiponso Koran alemba ndondomeko yofanana ya malamulo a Mulungu, kusiyana ndi yomwe yalembedwa ndi mpingo wa Aroma, womwe wasintha ena a Malamulowo. Lamulo lachiwiri loletsa kupembedza mafano osema walichotsa, lamulo la Sabata lafupikitsidwa ndipo silikutchulamo Mulungu Mlengi ndi tsiku lachisanu ndi chiwiri.



Lamulo lakhumi lagawidwa pawiri kulowa m'malo mwa lachiwiri walichotsalo poyesetsa kukwanitsabe chiwerengero khumi. Ngakhale izi zachitika, anthu onse abwerere ku malamulo a Mulungu, osasinthika. Ndi pemphero la mlembi wa kabukhuka kuti Mulungu akutsanulireni chisomo chake pamene mukuwerenga ndi kulingirira zokonzetsera khalidwe lanu kufanana ndi lake.

**Matanthauzo**: ***Allah***: Dzina la Chisilamu (chi-Arabu) kutanthauza Iye Wamkurukuru kapena Mulungu.

***Heathen***: Munthu amene samakhulupirira Mulungu wa m'Baibulo ndiponso Koran, iye amene si Mkhristu, Myuda kapena Msilamu. Werenganinso *World Book Dictionary*, Volume 1: Lofalitsidwa ndi Mlembi wa *World Book Encyclopedia*.

Chidziwitso choonjezera mungachipeze: www.salahallah.com

THE HOLY QUR'AN English Translation of Meanings and Commentary.

**Tumizani ndemanga ndi mafunso anu ku adiresi yomwe muli nayo pafupi:**

**TUMIZANI NDEMANGA NDI MAFUNSO ANU KU ADIRESI YOMWE MULI NAYO PAFUPI:**


**RLMedia**

32 Ceres Str, Comptonville, Johannesburg, South Africa

www.rlmedia.co.za

+27(0)836254786